# ISRAELI NDI MPINGO [3]

Kapena, Numeri, mutu wa 20 wa Numeri, ndi pamene tikhazikitsirepo mutu wathu usikuuno.

2 Ndipo tsopano ife tiri ndi Mabaibulo enanso foro, ngati aliyense akufuna kuti aphunzire limodzi nafe. Ena a ma eledara akhala osangalala kukubweretserani inu Mabaibulo foro owonjezera awa pano. Aliyense akufuna Baibulo, mungokweza dzanja lanu. Chabwino, apa pali ena cha apa. M'bale Fleeman, ngati inu mungabwere ndi kudzawatenga—mudzatenge ndipo muwapereke mpaka iwo athe.

3 Numeri, Numeri, mutu wa 20. Ife titenga "ulendo" uwu kuchokera ku Numeri posachedwapa, chifukwa ilo limafotokoza mwatsatanetsatane kuposa momwe Eksodo amaperekera, ndi nkhaniyo. Ndipo ife tikufuna kuti tiyambire pafupifupi ndime ya 7, ndipo tiwerenge.

> *Ndipo AMBUYE anayankhula kwa Mose, anati,*
>
> *Tenga ndodo, ndipo usonkhanitse msonkhano pamodzi, iwe, ndi Aroni m'bale wako, ndipo muyankhule inu kwa thanthwe pamaso pawo; ndipo ilo* lidzatulutsa *madzi ake,. . .*

4 Ine ndikufuna kuti inu muzindikire zimenezo, "Ilo lidzatulutsa Ake," dzina la munthu, "Madzi Ake."

> *. . .ndipo adzabweretsa kwa iwo madzi ochokera mu thanthwe: chotero iwe udzapereka kwa osonkhana ndi nyama zawo zimwe.*
>
> *Ndipo Mose anatenga ndodo pamaso pa AMBUYE, monga iye anamulamulira iye.*
>
> *Ndipo Mose ndi Aroni anasonkhanitsa* pamodzi *osonkhana pamodzi pamaso pa thanthwe, ndipo iye anati kwa iwo, Imvani tsopano, opanduka inu; tiyenera ife tikutungireni inu madzi kuchokera mu thanthwe ili?*
>
> *Ndipo Mose anakweza dzanja lake, ndipo ndi ndodo yake iye anakantha thanthwe kawiri: ndipo* madzi *anaturuka mochuluka, ndipo osonkhanawo anamwa, ndi nyama zawo aponso.*

5 Tsopano, palibe munthu ali woyenera kutsegula Mawu a Mulungu. Mu Baibulo, Ilo linati, kuti ngakhale "Mmodzi anabwera, ndipo monga Mmodzi wophedwa kuchokera ku maziko a dziko lapansi, Mwanawankhosa, ndipo Iye anali Mmodzi yekha Amene anali wokhoza kutenga Bukhulo, kuti amasule zisindikizo, ndi kutsegula Mawu." Tsopano Mzimu Woyera, umene Yesu anautumizanso mmalo Mwake, kuti udzakhale ndi ife mpaka Iye atadzabwera kachiwiri.

6 M’bale Neville, kodi inu mungaimirire ndi kumupempha Mulungu kuti akomane ndi ife tsopano, ndi kudalitsa Mawu Ake pamene Iwo akupita, ngati inu mungathe? Ndipo mulole . . . mumufunse Iye kuti abwere ndi kudzatithandiza ife tsopano kuti tifotokoze Mawu Ake.

7 Pamene ife tikuweramitsa mitu yathu, ngati inu mungathe, mu mawu a pemphero.

8 [M’bale Neville akupemphera, “Atate athu, kachiwiri usikuuno, ife tikubwera pamaso Panu mu kudzichepetsa koona, Ambuye, pozindikira kuti kukwanira kwaumunthu ndi kosakwanira kukwaniritsa zosowa zauzimu za gulu ili kuti Inu mwasonkhanitsa pamodzi mwa Mzimu Woyera—Mkonzi]. Zoonadi, Ambuye!

[Ndipo, Atate, pamene ine ndaima pano usikuuno, mkhalapakati, osati mwa chigamulo changa, koma mwa kusankha Kwanu, eledara wa Mpingo wa Ambuye Yesu Khristu, mwa ulamuliro wa Mzimu Woyera,] Hmm! [Ine ndikukupemphani Inu, mu Dzina la Yesu, usikuuno, kuti muyang’ane pa ife, mu . . . mu mlingo umenewo wa chifundo,] Inde, Atate. [momwe ife tingakhoze kupeza chisomo pamaso Panu. Ndipo uyu, m’bale wanga ndi woyenda mzanga ndi mtumiki mzanga,] Inde. [yemwe Inu munamuitana kuchokera mmimba ya amayi ake, Atate, akhoze kukhala wokhoza, usikuuno, kuti atsegule Lemba, mwa Mzimu Woyera.] Perekani izi, Ambuye.

[Ndipo monga mmodzi yemwe ali woyang’anira gulu lalikulu ili,] Perekani izi, Ambuye. [Atate, osati kuyankhula mochuluka apa . . . koma chifukwa cha kukonderedwa kumene ife tapeza kudzera mwa Mwana Wanu wopachikidwa, usikuuno,] Inde. [yang’anani pa ife, ndipo mutibatizenso ife ndi mphamvu yotsitsimutsa yochokera Kumwamba,] Perekani izi, Ambuye. [mutsegule malingaliro athu ku Lemba, ndipo mulole mitima yathu itenthe mkati mwathu pamene ife tikuyanjana limodzi, zokhudza zinthu izi zimene Inu mwazipereka.] Inde, Atate.

[O, Atate athu, usikuuno, tsopano mutilole ife tikhazikike, Mulungu Wamkulu, mu mzimu wosinkhasinkha, pansi pa denga lodala la Kumwamba usikuuno, chezerani anthu Anu, tiphunzitseni ife kuchokera mu Mawu. Oh, phunziro lirilonse—lingaliro lirilonse lomwe lingakhale lofalitsidwa, usikuuno.] Inde. [Mulungu Wamkulu, mukhazikitse malingaliro athu,] Ameni. [ndipo tipatseni ife mdalitso wodabwitsa usikuuno.] Perekani izi, Ambuye.

[Ndipo tsopano, Atate, pakuti zonse izi ife tikupempha, mu Dzina la Yesu, ife tikukupatsani Inu matamando ndi ulemu ndi ulemelero chifukwa cha zimenezo. Ameni, ndi ameni]. Ameni. (Zikomo inu, M’bale.)

Pakhoza kukhala kuti pali mlendo pakati pathu, ameneyo ndi m'busa wathu pano, M'bale Neville.

9 Iye wasasa mawu pang'ono pa mmero wake, ndipo ndicho chifukwa chake ife sitinamve zambiri za iye mausiku angapo apitawa. Iye anakhalangati wafunsidwa kuti akhale chete momwe angathere, pa chifukwa chimenecho, mpaka mmero wake utakhala nawo mwayi kuti—kuti—kuti . . . iye akhalenso ndi mwayi wokhalanso bwino.

10 Tsopano, ife takhala tikuphunzira Bukhu la Eksodo. *Eksodo* ndi "kuyitana atuluke, kwa ana a Mulungu." Iwo anali anthu a Mulungu nthawi yonse imene iwo anali ku Igupto. Koma pamene anadzakhala ndi eksodo yawo, iwo anadzakhala mpingo wa Mulungu, pakuti mpingo, mawu akuti *mpingo*, amatanthauza "oyitanidwa atuluke." Ndipo ife tikukhulupirira kuti tiri pafupi ndi eksodo usikuuno. Inu mukukhulupirira zimenezo? Ife tiri pafupi ndi eksodo ina, kuitana atuluke, kulekanitsa, kukonzekera.

11 Tsopano, ine ndikukhulupirira ine ndiri, ine ndimakonda, ndipo ndakhala ndikuimbidwa mlandu, ndipo ndi chimene ine ndiri, wofanizitsa, chifukwa ine ndimakhulupirira kuti zinthu zakale zonse zinali mthunzi wa zinthu zimene zinali nkudza. Lemba limaphunzitsa zimenezo. Ndipo ngati ife tingakhoze kukhala ndi masomphenya ena, ndi kuyang'ana chimene Chipangano Chakale chinali, ife tiwona chimene Chipangano Chakale chiri, kapena chimene Chipangano Chatsopano chiri, kani. Mwaona, choyimira. Iwo anali a mithunzi ndi zitsanzo, kuti ife tidzakhoze kudziwa choti tichite. Onani momwe iwo anagwera ndi momwe iwo anawukira, ndi chimene iwo anachita pamene iwo ankatumikira Mulungu, ndipo izo ziri ngati mthunzi kwa ife.

12 Tsopano, usiku woyamba, Lachitatu usiku, ife tinatenga "mpingo," kuti tipeze, kwenikweni, chimene mpingo unali. Ndipo tsopano mu msonkhano wamachiritso . . . Ndipo iyi ndi nthawi yoyamba yomwe ine ndakhalapo ndi chitsitsimutso mu zaka seveni, cha mtundu uwu. Zaka seveni, sabata ikubwerayi, ine ndinachoka ku kachisi ndi kupita kunja mmisonkhano yokopa anthu ya ulaliki, ya misonkhano ya machiritso.

13 Ndipo ine ndazipereka izo kwa mamanenjala omwe amapanga zolalikira, nthawizambiri, ndipo ndimangoyankhula pa phunziro la machiritso Auzimu, chifukwa ife tinali omvetsera osakanizika, a—a Achimethodisti, Abaptisti, Apresbateria, Akatolika, Achiorthodox, Achiyuda, chirichonse. Ndipo nthawizina ngati uponda pa kuphunzitsa kwa zachipembedzo za anthu, izo zingawapangitse atumiki kuwaletsa anthu kuti asabwere ku tchalitchi, ena a iwo amene amafunikira kwenikweni kuti abwere kuti adzapempherer edwe. Chifukwa chake ine ndinangotsekera pa chirichonse kupatula kuphunzitsa

kwakukulu kwa uvangeli, kwachikhazikitso cha Baibulo, imfa, kuikidwa mmanda, ndi chiukitsiro cha Khristu; inu mukudziwa chimene chiphunzitso, cha chikhazikitso cha uvangeli chiri.

14 Koma tsopano mu kachisi muno, ku mpingo wanga wawung'ono umene Ambuye anandipatsa ine zaka twente zapitazo, Ine—ine ndimakhala womasuka kuti ine ndikhoza kuphunzitsa chomwe kukhudzidwa kwanga kuli. Ndiyeno, ndipo ife tiribe umembala uliwonse pano, ife timangokhala ndi chiyanjano chimodzi ndi . . . Ndinu membala pano pamene inu muli pano usikuuno, ndinu membala. Ife tiribe aliwonse—mamembala aliwonse, chiyanjano basi.

15 Ndipo ife tsopano, mkati muno, inu mukhoza kupeza zinthu zomwe inu mukuti, "M'bale Branham, ine sindikugwirizana nazo Izo."

16 Chabwino, tsopano, ngati inu simutero, inu mutero, inu mugwiritse ntchito njira yomweyo ine ndimachitira ndikamadya chitumbuwa chachikulu cha nthudza ndi kapeza nthangala. Ine sindimasiya kudya chitumbuwa cha nthudzacho; kungoti ine sindimadya nthangalayo. Ine ndimangotaya nthangalayo ndi kumapitirira kumadya chitumbuwa cha nthudzacho. Kapena pamene iwe ukudya nkhuku, iyo imayenera kukhala ndi fupa mmwendo wake, inu mukudziwa. Kotero musataye nkhukuyo chifukwa inu mwagunda fupa, mungotayira fupalo kutali. Ndi zomwe inu mukuganiza kuti ziri ndi fupa kapena . . . chabwino, inu mungochitaya icho tsopano, ndipo inu mutenge chimene inu mukuganiza kuti chiri cholondola.

17 Tsopano, ife tikupeza kuti Mpingo wa Mulungu si chifuniro cha anthu. Ndi chisankho. Chisankho chimakhala mwa Mulungu. Mulungu anamuitana Abrahamu, woyambitsa wa chikhulupiriro, woyambitsa. Mulungu anali Woyambitsa, ndithudi. Koma Abrahamu, pachiyambi, anaitanidwa atuluke kuchokera ku Kaldia, mzinda wa Uri, kuchokera mu zidikha za Shinara, osati ndi ubwino wake uli wonse. Mulungu anamupulumutsa iye, mopanda mangawa, ndipo anamupatsa iye lonjezo la Mbewu yake yonse, mopanda mangawa.

18 Yesu, pamene anadza, Iye anati, "Palibe munthu angakhoze kubwera kwa Ine kupatula Atate Anga atamukoka iye." Inu munalibe kanthu kokhudza za kubwera kwa Mulungu, ndiye. Mulungu anakukokerani inu kwa Yesu. "Ndipo onse amene adza kwa Ine, Ine mwanjira iliyonse sindidzawatayira kunja. Iye amene amva Mawu Anga ndi kukhulupirira pa Iye amene ananditumа Ine, ali nawo Moyo wosatha; ndipo sadzabwera ku chiweruzo, koma wadutsa kuchokera ku imfa wapita ku Moyo. Iye amene adya Thupi Langa ndi kumwa Magazi Anga, ali nawo" tensi yatsopano "Moyo wosatha, ndipo Ine ndidzamuukitsa iye mmasiku otsiriza." Ndi zomwe Iye ananena, kotero ine

ndikungobwereza Mawu Ake. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti izo ndi Choonadi.

19 Chotero, ine ndikukhulupirira kuti Mulungu anapereka zitsanzo. Iye anamupulumutsa Abrahamu, mopanda mangawa.

20 Iye anapangana pangano ndi munthu, ndipo munthu nthawizonse amaswa pangano lake. Koma munthu nthawizonse wakhala akuyesetsa kuti apeze njira ina yoti adzipulumutsire yekha, kuyesetsa kuti adzipange yekha. Izo zimachokera ku kupysinjika: Mmunda wa Edeni, pamene munthu anazindikira kuti iye anali atachimwa, iye anayesetsa kudzipangira yekha chipembedzo, chophimba. Mawu akuti *chipembedzo* amatanthauza "chophimba." Ndipo Adamu ndi Eva anasoka masamba a mkuyu pamodzi, ndipo anadzipangira okha chipembedzo. Ndipo kuyambira pamenepo chakhala chiri kupsyinjika kwa munthu kudutsa mu m'badwo, kuyesetsa kuti achite chinachake kuti adzipulumutse yekha.

21 Koma iwe umapulumutsidwa mwa chisomo, kusankhidwa, kudziwiratu kwa Mulungu, kukonzedweratu, kudzodzedweratu. Paulo akuuza mpingo wa ku Efeso kuti, "Mulungu anatikonzeratu ife mwa Khristu asanaikidwe maziko a dziko lapansi." Taganizani za zimenezo! "Anatikonzeratu ife mwa Khristu asanaikidwe maziko a dziko lapansi." Bwanji ife timadandaula ndiye? Chokani ku kudandaula, ife ndife zolengedwa zokondwa kwambiri zomwe inu munayamba mwaziwonapo. Mai, inu mungakhulupirire bwanji zimenezo ndi kuleka kukhala wokondwa?

Ine ndinkakonda kumuwona M'bale Bosworth wachikulire, ndipo iye anati, "M'bale Branham!"

Ine ndinati, "Kodi inu mukupeza bwanji mmawa uno, M'bale Bosworth?"

Anati, "Vuto lakale lomwelo labwerera pa ine, M'bale Branham."

Ine ndinati, "Vuto lakale lomwelo, ndi chiyani ilo?"

Anati, "Basi wokondwa kwambiri, ine ndikulephera kugona!" Ine ndinati. . .Iye anati, "M'bale Branham, ine ndingakhoze bwanji kukhulupirira zomwe ine ndimakhulupirirazi, nkumalephera kukhala wokondwa?" Mwaona, izo nzoona.

22 Inu mukudziwa kuti Khristu anatenga kale malo anu ngati wochimwa. Iye anafa. Mulungu anamuvomereza Iye. Iye anauka kachiwiri, akukhala padzanja lamanja la Ufumu Wake. Mulungu anati, "Uyu ndi Mwana Wanga wokondedwa mwa Yemwe Ine ndikukondwera, mvereni inu Iye." Ndipo ndi Uyo pamenepo Iye, a—Khomo, Chipata, Njira, Choonadi, Moyo.

23 Ndipo ife timalowa bwanji mwa Iye? Iye ndi Mpingo. Mpingo uli nawo Moyo wosatha, iwo unadzozedweratu kale

kuti udzawonekere wopanda banga kapena chilema. Mulungu ananena kale kuti izo zikanadzakhala pamenepo, izo zidzakhala ziri pamenepo! Tsopano, Mulungu ananena chomwecho. Kotero ndiye ife timalowa bwanji mu Mpingo? Mwa umembala umodzi? Ayi. Mwa kugwirana chanza ndi winawake? Ayi. Mawonekedwe ena kapena uba-...? Ayi. "Mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi limodzi, ndi kudzakhala ziwalo za Thupi limenelo." Akorinto Woyamba 12 amati, "Mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi limodzi, ndi kukhala ziwalo za Thupi limenelo." Ndi motani? Ubatizo wauzimu umene umatilowetsa ife mu Thupi la Khristu, ndipo zikatero timadzazidwa ndi Mzimu wa Mulungu.

24 Kusindikizidwa mpaka motalika bwanji? Aefeso 4:30, "Musawukwiyitse Mzimu Woyera wa Mulungu umene inu munasindikizidwa nawo mpaka tsiku la chiwombolo chanu." Osati kuchokera ku chitsitsimutso chimodzi kupita ku chimzake; koma, "mpaka tsiku la mawomboledwe anu." Ameni. Moyo Wosatha! *Wosatha* si pang'ono chabe...danga la nthawi, wosatha ndi "Wamuyaya nthawizonse," sangakhoze kufa monga momwe njere ya chimanga ingakhoze kudzakhala chisoso.

25 Ndipo ngati munthu wabadwa mwa Mzimu wa Mulungu, basi pomwepo iye amakhala Moyo. Monga ine ndinanena usiku wina, kumwa, kusuta, njuga, kumwa, kutukwana, kulumbira, izo si tchimo, ndi zikhumbo za tchimo. Ndi chifukwa chakuti ndiwe wochimwa, chifukwa chimene zinthu zimenezo zimabwerapo. Koma ngati ndiwe wokhulupirira, zinthu zimenezo sizingakhoze kubwera, chifukwa madzi owawa ndi okoma sangabwere kuchokera pa kasupe mmodzi. Chisoso chikhoza. Mbewu ya tirigu siyingakhoze kubala chisoso, chifukwa chikhalidwe cha iyo ndi tirigu. Iyo iyenera kubereka chimene iyo ili. Ndipo ngati Mzimu Woyera uli mkatimo, iwo umabereka Moyo wa Khristu. Ameni. Ndicho chikhulupiriro. Ameni. Chabwino.

26 Tsopano, ndiye ife tikupeza kuti, ife tikuyang'ana mithunzi tsopano. Ndipo ife tikupeza, ndiye, ndipo Mulungu anatipatsa ife chitsanzo, Khristu mwa mmodzi aliyense wa mbadwa, kapena kutsika kudutsa m'badwo. Mwa Abrahamu, Mulungu anali ndi kusankha. Mwa Isaki, kulungamitsidwa, kuyitana.

27 Mulungu anamuitana Isaki ngakhale iye asanabadwe nkomwe, anamupatsa iye dzina lake, chirichonse, monga momwe Iye anachitira ndi Yesu. Ndiye ine ndikuzindikira Isaki mwangwiro...Ife tinalibe nthawi kuti tigwire zimenezo, koma kodi inu munazindikira Isaki, mwana mmodzi yekhayo wa abambo ake, kupyolera lonjezo, ananyamula nkhuni kumakwera nazo phiri lomwelo, atanyamula, anammanga manja ake, anakaperekedwa ngati nsembe. Ndipo pamene iye anayamba kutenga moyo wa mwana wake yemwe, Abrahamu, kanyama kakang'ono kanalira, kankhosa kakang'ono, mwana

wa nkhosa, atamangiririridwa, anagwidwa mu chipululu, ndi nyanga zake. Ndipo Mzimu Woyera ukufuula kuchokera Kumwamba, "Chotsa dzanja lako." Ndipo iye anapita ndipo anakamutenga mwanawankhosayo ndi anakampereka mmalo mwake; amene anali Mwanawankhosa wophedwa kuchokera ku maziko a dziko lapansi. Ndi zimenezotu pamenepo, chithunzi chokongola.

28 Kuitana, kusankha, mwa—mwa Abrahamu. Kulungamitsidwa, mwa Isaki. Chisomo, mwa Yakobo. Aliyense amene anawerengapo moyo wa Yakobo, akudziwa kuti iwe ukuyenera kukhulupirira mu chisomo. Ndi chisomo, mwa Yakobo. Ndipo ungwiro, mwa Yosefe, palibe chomutsutsa iye, mu Baibulo; munthu wangwiro, wangwiro wa Khristu. Ndiye ife tikupeza kuti mbadwa zonse zinapita uko ku Igupto, ndipo kumeneko iwo anakakhala. Ndipo mafuko awo anaphuka ndipo iwo anaphimba—maiko, chifukwa Mulungu analonjeza izo kwa Abrahamu.

29 Mawu a Mulungu nthawi iliyonse amayenera kukwaniritsidwa. Magudumu a ulosi wa Mulungu amazungulira pang'onopang'ono, koma motsimikiza. Ngati uchita zolakwika, iwe umaganiza kuti ukupitirira nazo. Koma ingokumbukirani, mnyamata kapena mtsikana, izo zidzazungulira mpaka pakhomo pako limodzi la masiku awa. Iwe udzadabwa kuti ndi liti ndipo motani, koma izo zidzakhala pamenepo. Udzakolola zimene wabzala, nthawi iliyonse. Mulungu anayankhula izo, izo ziyenera kukhala chomwecho. Kuti, "Mawu Anu anakhazikika Kumwamba kwanthawizonse." Iwo ananenedwa kale. Iwo samatsutsana zokhudza Iwo kumwamba uko; izo zinakhazikika kale. Ife timatsutsana za Iwo. Koma, mu Ulemelero, Iwo ndi okhazikika. Pamene Mulungu anena chirichonse, icho chiyenera kukhala. Chabwino, kodi izo si zodabwitsa?

30 Kodi inu simungakhoze basi kuzikhazikitsa izo mu mtima mwanu usikuuno? "Ambuye Yesu, ine ndikukukhulupiririrani Inu. Izo zikukhazikitsa izo. Aleluya! Ine ndikubwera tsopano, ine ndikufuna Inu kuti mundipatse ine ubatizo, Mzimu." Ndipo inu muwupeza Iwo apo pomwe. Chabwino. Ndiye, kwanthawizonse, Mulungu adzakusindikizani inu mwa Mzimu Woyera mpaka tsiku la chiwombolo chanu. Chabwino.

31 Ndiye ife tikuzindikira, mu phunziro la usiku wotsatira, ife tikupeza Yosefe akutchula za mafupa ake. Ndipo momwe iye anaimiridwa mwangwiro mwa Khristu, ngakhale mpaka mwinjiro wake, chirichonse.

32 Chirichonse mpaka pano chinakwaniritsidwa mwangwiro mwa Khristu. Zindikirani. Iye anali Munthu wotsiriza, Nsembe yotsiriza ya Mbewu ya Abrahamu. Ife tinazipeza zimenezo (sichoncho ife?) pamene iye anapanga nsembe pa phiri, ndipo Kuwala kwakung'ono kunapita pakati pa izo

ndi kukatsimikizira lumbirirolo. Ndipo Mulungu anayima pamenepo ndipo anapanga lumbiriro pa Kalvare, Iye anatenga lumbiriro ndipo anang'amba Lemba, kapena kulemba, anang'amba, anatenga gawo limodzi, monga ife tinazipeza izo mmasiku amenewo njira yopangira pangano.

33 Monga, ife lero timagwirana chanza. Ku India, kapena ine ndikukhulupirira ndi China, iwo amathirana mchere pang'ono pa wina ndi mzake. Ndipo nthawi zambiri iwo amapatsana mwana kwa wina ndi mzake, mwa chitsimikizo cha lumbiriro.

34 Koma mu nthawi za kummawa iwo ankalemba izo pa pepala, ndipo ankapha chinyama, ndipo ankaima pakati pa zidutswa zakufa za chinyamacho, ankang'amba chidutswa cha pepala, pamodzi, nkuchipereka icho kwa wina aliyense. Ndipo pamene izo zibweretsedwa pamodzi, chidutswa chirichonse cha pepala limenelo chimayenera kulumikizana ndi chimzake.

35 Zokongola! Mulungu anamutenga Khristu, pa Kalvare, anamung'amba Iye pakati, Solo ndi Thupi. Iye analitumiza ilo, Thupilo, mmwamba ku dzanja Lake lamanja, ndipo anatumiza Mzimu Woyera kubwerera. Pangano ndi anthu! Ndipo iwe umakhulupirira, mwa chikhulupiriro, monga Abrahamu anachitira, ndipo iye anapatsidwa chisindikizo cha mdulidwe kwa chitsimikiziro cha chikhulupiriro chake. Ndipo iwe umakhulupirira ndi kumulandira Yesu ngati Mpulumutsi wako, kenako Mulungu amakupatsa iwe ubatizo wa Mzimu Woyera monga chitsimikiziro cha chikhulupiriro chako.

36 Inu mukuti inu "ndikukhulupirira, ndipo sindinalandire Mzimu Woyera"? Chinachake chalakwika ndi chikhulupiriro chanucho. Mulungu amadula mtima miniti yomweyo imene wokhulupirira abwera mu kugonjera kwathunthu. Ameni. Amati, Iwo, chabwino, ndithudi ndikanachita chinachake, ine ndinachimverera icho ngakhale kubwereranso. Mukumvetsa izo! Pamene wokhulupirira...Ndi izi tsopano! Pamene wokhulupirira akhulupirira kwenikweni pa Ambuye Yesu Khristu, Mulungu amakhala wokakamizidwa kuti amupatse iye Mzimu Woyera. Chitsimikizo cha chikhulupiriro chake! Mukuti, "Chavuta ndi chiyani, M'bale Branham?" Chikhulupiriro chako chokha, ndizo zonse. Ngati ukhulupirira moona, Mulungu amakhala pamenepo kuti apereke Iwo kwa iwe.

37 "Pamene Petro anali kuyankhula Mawu awa, Mzimu Woyera unagwera pa iwo amene anamva Mawu." Ndi kulondola uko? Machitidwe 10:49. Chabwino, zindikirani, Mzimu Woyera ndi Moto zinabwera kuchokera Kumwamba, zinadzawotcha litsiro lonselo, zinadzapanga mdulidwe mtimawo, kudula zotsalira zonse, ndi kukhala cholengedwa chatsopano.

38 Tsopano, ndiye ife tikupeza kuti zitatha zaka foro handiredi...Usiku wathawu ife tinali ndi choyimira cha mbadwa. Tinabwereranso pakati pa mizere ndi kukawona

chifukwa chimene iwo ankafuna kuti akayikidwe mu—mdziko lolonjezedwa. Kodi inu munazikonda zimenezo? Munasangalala nazo? Bwanji, tsopano izo sizinalembedwe apo pomwe, koma inu mukuziwona izo.

39 Monga ife tinali kuyankhula za Abrahamu, ndi momwe Mulungu anamutengera Sarah ndi Abrahamu pamene iwo anali usinkhu wa zaka handiredi, ndi kuwatembenuzira iwo kukhala mnyamata ndi mtsikana kachiwiri, ndi kuwapatsa iwo mwana uyu. Izo zinali ngati zovutirapo kuziwona, poyamba. Koma inu mutayang'ana pa Malemba, kuyang'ana pansi apo ndi kupeza chimene chinachitika, inu muwona kuti ndi Choonadi. Kodi Iye anali kuchita chiyani? Kutsimikizira Mawu Ake, kuti tsiku lina, ife amene tinakalamba ndipo tinachita imvi ndi makwinya, tsikulina ife tidzabwereranso kudzakhala mnyamata ndi mtsikana kachiwiri. Mulungu anatipatsa ife moyo, ndipo tafika pa kukhwima, imfa inadzalowamo, inadzatitengera ife kutali. Koma zonse zomwe imfa ingakhoze kuchita ndi kutitengera ife kutali, zikatero iyo yatha. Ndiye zonse—gawo lakale lokayikira ndi chirichonse, ziri ngati moyo wa munthu mmenemo watulukamo, ndiye palibe chomwe chatsalira koma ungwiro. Chimene thupi ili linali pamene ilo linali mu ungwiro, chimene Mulungu ankafuna pamene ilo lidzauke mu chiukitsiro, ilo lidzakhala ungwiro. Ameni. Oh, pamene ine ndiganiza za zimenezo, mtima wanga umangotembenuzika! Eya. Iwo si maloto a nthano chabe. Ndi PAKUTI ATERO AMBUYE! Mulungu ananena chomwecho, ndiye ine ndidzakhazikitsa moyo wanga pamenepo. Inde, bwana. Mulungu ananena chomwecho, izo zikukhazikitsa izo kwanthawizonse. Uh-huh. Izo zakhazikika Kumwamba, ndipo ngati kachidutswa kakang'ono ka Kumwamba kali mu mtima mwathu, izo ziyenera kukhazikitsa izo pamenepo. Ndizo zonse. Izo zimangopangitsa izo zonse kukhala bwino. "Mulungu, Inu munanena chomwecho. Ine ndikukhulupirira Izo, ndipo ndizo zonse, izo ndi zokwanira."

40 Tsopano, tsopano ife tikuwabweretsa iwo pansi basi ulendo usanafike. Ndipo ife tikupeza apo kuti pamene Mose (ife tinazipeza izo usiku wathawu) akubwera uko kudzaweta nkhosa za Ayatero, ndipo ife tinafika podzapeza kuti Mulungu anayankhula ndi iye. Ndipo Mose ankafuna kuti awone Ulemelero Wake. Ndipo Mulungu anamusonyeza iye Ulemelero Wake, ndipo uko kunali kuchita zozizwitsa, ndi machiritso Auzimu. Ndi kulondola uko? Uwo uyenera kukhala Ulemelero wa Mulungu. Kuyankhula za Ulemelero wa Shekinah, ife tiyenera kukhala nawo Iwo usikuuno!

41 Ndipo, m'bale, ife tiri, Chikhristu chonse, chikuyembekezera Kudza kwa Ambuye ndi Mkwatulo wa mpingo, onse amene ali ndi chidziwitso chirichonse cha Mawu. Chabwino, ngati ife sitingakhoze kukhala nacho chikhulupiriro chokwanira cha machiritso Auzimu, ife tingakhale nacho bwanji chikhulupiriro

chokwatulitsa? Oh, ine ndikukhulupirira pali mayitanidwe aakulu amene akubwera. Ine ndikukhulupirira monga Davide ananena, iye anagona pamenepo ndipo anadikirira mpaka, iye anamvetsera ndi kuyembekezera. Patapita nthawi anamva mphepo yamkuntho ikudutsa mmasamba a mabulosi, ikuzungulira zungulira. Iye anadziwa kuti Mulungu anali kupita patsogolo pake. Oh, m'bale, ine ndikumvetsera mkokomo wa masamba, phokoso mu tchire la mabulosi. Mulungu akupita patsogolo pa nkhondoyo, ndiye tiyeni tidzuke ndi kuvala zida zonse za Mulungu, kusolola lupanga, kupita motsatira izo! Nkhondoyo ndi yathu, ndiye. Pamene ife tiwona dzanja la Mulungu likusunthira chitsogolo, kupyolera mu zizindikiro ndi zodabwitsa, tiyeni tiyambe kutsatira.

42 Tsopano, kenako, ife tikupeza kuti Mose anatanganidwa kwambiri ndi ntchito yake ya ubusa, ndipo iye anaiwala chinachake. Chinthu chofunikira kwambiri chimene iye—chimene iye—chimene iye ankayenera kuti achichite, iye anayiwala. Iye anali akumutenga, usiku womwewo wa chiwombolo, iye anali akumutengera mwana wake ku Igupto, wosadulidwa. Ndipo Zipporah. . .Mulungu akanamuphera iye mnyumba ya alendo, koma Zipporah anamudula mwanayo. Chisindikizo cha pangano, inu mukuchiwona icho? Pasanakhale chiwombolo, munthu aliyense ayenera kukhala mu pangano, chifukwa Mulungu ali ndi pangano lero. Ndipo kotero Zipporah anamudula mwanayo, pangano, ndipo anabweza mkwiyo wa Mulungu.

43 Ndipo, abwenzi, lero, tonsefe tiri ndi zitsitsimutso zazikulu, kapena kuyesetsa kuti tikhale nazo, koma ife tikuyiwala Chisindikizo cha Mulungu cha pangano, Mzimu Woyera, Mwala wokanidwa, womwewo. . .Mtondo umene umasakaniza ndi kumata zidhina pamodzi. Kodi ife tingachite motani izo popanda Iwo? Mulungu anati, "Izo zikanadzachitika kuti Ine ndidzalemba malamulo Anga pa magome a mitima yawo. Langizo likhale pa langizo, mzere pa mzere, apa pang'ono ndi apo pang'ono. Gwiritsitsani kwa icho chimene chiri chabwino. Ndi milomo yachibwibwi ndi malirime ena ine ndidzayankhula kwa anthu awa, ndipo uwu ndiwo Mpumulo." Yesaya 28. "Izi zonse iwo sakanakhoza kuzimva; anatembenuka, akupukusa mutu wawo." Munthu akumenyera njira yake yopita ku chiwonongeko!

44 Ndiye ife tikupeza kuti mkwiyo wa Mulungu utatha kuchotsedwapo, iwo ali uko mu Igupto tsopano kuti akawombole ana a—a Israeli. Ine ndikuganiza uwu ndi mutu wokongola. Ine ndiyenera kuwerenga zina chabe za izo, mulimonse, ngati ife sitifika kwa zonse za izo. Mutu wa 12, tiyeni tiyambire tsopano, wa Eksodo 12, kuwerenga, ndi kufulumira motsatira kumene. Ine ndiyesetsa kuti ndisakutopetseni inu, chifukwa ife tiri nayo nthawi yayitali yoti tipitebe.

*Ndipo* A*mbuye* *anayankhula kwa Mose ndi* kwa *Aroni*. . .

45 Ine ndidikirira kamphindi chabe kuchitira kuti inu mutsimikize kuti mwapeza kuwerenga kwa Lemba. Pakuti, ngati mutaphonye izo. . .Zoyimira zokongola chomwecho! Ine ndikuzikonda izi. Tsopano, apa pali nsembe yomwe ife titi tiyankhulepo tsopano.

46 Tsopano, iwo amakhala ndi mliri pambuyo pa mliri, Mulungu anali atachita mitundu yonse ya zozizwitsa ndi zizindikiro. Oh, momwe ine ndikanafunira kukwera pamenepo kwa kanthawi pang'ono! Mulungu, basi usiku wa chiwombolo, anayamba kusonyeza zizindikiro ndi zodabwitsa ndi zozizwitsa. Mwaona, Mulungu nthawizonse amakhala tensi ya moyo. Iye anamuuza Mose, "INE NDINE." (Ayi "Ine ndinali" kapena "ine ndidzakhala.") "INE NDINE" tsopano, tensi yatsopano. Ndipo Iye ali yemweyo INE NDINE usikuuno. (Osati "Ine ndinali kumbuyo uko.") "INE NDINE!" Mngelo wa Pangano, akadali yemweyo dzulo, lero ndi kwanthawizonse, Mngelo yemweyo.

Zindikirani tsopano, apa pali chotsiriza.

47 Iwo anali ndi utitiri, anali ndi ntchentche, anali ndi zithupsya. Ndipo, ine ndikufuna kuti inu muzindikire, iwo anali ndi otsanzira. Yambre ndi Yane, akuyesetsa kuti awatsutse iwo, amachita zinthu zomwezo zomwe iwo anali kuchita, mpaka izo zinapita nthawi yotalika kwambiri. Mwa kuyankhula kwina, iwo anali kulalikira Uthenga, iwo anali akupita limodzi nawo kuyesera kumatsanzira Mose ndi Aroni. Koma ine ndikufuna kuti inu muzindikire chinthu china. Ngati inu amene muti muwerenge tsopano, pamene ife tinasiyira usiku watha, kuyambira pa mutu wa 6 mpaka wa 12. Amatsenga awa, iwo amakhoza kubweretsa zinthuzo, koma iwo samakhoza kuzichotsa izo. Inu mukuzindikira?

48 Anali ndani munthu uja tsiku lina, akuyesetsa kuti azichotsamo mu Baibulo, ponena kuti, "Mdierekezi akhoza kuchita zozizwitsa za machiritso"? Uko nkulakwitsa.

Mulungu anati, "Ine ndine Ambuye Mulungu wako Amene ndimachiritsa nthenda zako zonse."

49 Yesu anati, "Ngati nyumba igawanika pa iyo yokha, ngati Satana atulutsa Satana, ndiye ufumu wake wagawanika." Musamamunyozetse mdierekezi. Izo nzoona, iye ndi wanzeru kwambiri pa zimenezo. Satana sangadziponyere yekha panja. Iye amangokusokonezani inu, ndizo zonse. Ayi, bwana, Satana sangakhoze kutulutsa Satana.

Ine kuziponyera ndekha panja? Bwanji, ine ndikudziwa bwinoko kuposa zimenezo.

50 Zindikirani, ndipo inu musamupeputse Yesu Khristu, ngakhalenso, chifukwa Iye ndi Mphamvu ya pa mphamvu

zonse. Musamachite mantha ndi Satana, bola ngati inu muli mwa Iye. Koma ngati inu simuli mwa Iye, inu kulibwino muzinjenjemera. Koma ngati inu muli mwa Iye, osati ngakhale imfa yomwe ingakupwetekeni inu. Ndinu omasuka ku mantha onse. Oh, pamene ine ndiganiza za zimenezo, ine ndimafuna kufuula "Aleluya!" Ameni. Chabwino.

51 Tsopano ife tikufika ku mliri wotsiriza, chinthu chotsiriza. Mulungu anati, "Ine ndatopa ndi kupusitsidwa tsopano. Ine ndipereka mliri wotsiriza." Tsopano ine ndikufuna inu muzindikire, mliri wotsiriza unali imfa.

52 Tsopano, ife takhalapo nazo zivomezi, ife takhalapo nazo nkhondo ndi mphekesera za nkhondo, ife takhalapo nawo mafunde amphamvu, monga Yesu ananena kuti zikanadzakhala, nyanja ikubuma, mitima ya anthu ikulephera, vuto la mtima lochuluka (nthenda nambala-wani), mantha, kudodoma kwa nthawi, nsautso pakati pa mafuko, magalimoto mmisewu yotambalala, zinthu zonsezi zinakwaniritsidwa. Koma mliri wotsiriza ndi imfa; osati kuyankhula mwathupi, koma kuyankhula mwauzimu.

53 Imfa, mwauzimu, mu mpingo. Inu mukuzindikira iyo inali pakati pa ana, imfa yauzimu. Mpingo uli nawo mamembala ochuluka kuposa omwe iwo unayamba wakhalapo nawo, ukuchita bwinoko kuposa momwe iwo unayamba wachitirapo, ndipo komabe wofowoketsetsa mu mzimu momwe unayamba wakhalirapo. Izo nzoona. Ndizo basi monga izo zinali mu Igupto. Tsopano zindikirani chinthu chotsiriza.

54 Koma asanati, (oh, ameni) Mulungu asanalole kuti imfa yauzimu ivumbe, Iye anapanga njira yopulumukira kwa iwo amene ankafuna kutero. Aleluya! Oh, momwe ine ndikukondera zimenezo, Mulungu akukonza njira yopulumukirapo kwa iwo amene ankafuna kuti ayende mwa iyo. Tsopano, iwo amene sanafune, chabwino, iwo—iwo anatenga imfa.

55 Zindikirani tsopano mutu wa 12, ndime ya 1, Mose.

> *Ndipo* A*MBUYE* *anayankhula ndi Mose ndi Aroni mu dziko la Igupto, anati,*
>
> *Mwezi uno ukhale kwa inu chiyambi cha miyezi: iwo udzakhala mwezi woyamba wa chaka* kwa *inu.*
>
> *Yankhulani inu kwa osonkhana onse a Israeli, kuti, Pa tsiku la teni la mwezi uno iwo adzitengere kwa iwo munthu aliyense mwanawankhosa, molingana ndi nyumba ya makolo awo, mwanawankhosa kwa nyumba:*
>
> . . .*ngati* nyumba *ili yaing'ono kwambiri kwa mwana wa nkhosa, mumulole iye ndi woyandikana naye wa pafupi* ndi *nyumba yake atenge izo molingana ndi chiwerengero cha miyoyo; munthu aliyense*

*molingana* ndi *kudya adzapanga kuwerenga kwa mwanawankhosa.*

*Mwanawankhosa adzakhala wopanda chilema,* (zokongola bwanji!), *mwamuna...chaka choyamba—chaka choyamba:* (penyani) *inu muzitenga izo* kuchokera pakati *pa nkhosa,* ndi...*mbuzi:*

*Ndipo inu mudzaisunga iyo mpaka tsiku la fortini la mwezi womwewo: ndipo a*...(amenewo angakhale masiku foro), *ndipo gulu lonse la osonkhana a Israeli azaipha iyo madzulo.*

56 Penyani choyimira. Mwanawankhosa, kuyankhula mophiphiritsa, Mwanawankhosa wa Mulungu, Chitetezero chisanachitike chiwonongeko. Zindikirani, iye ayenera kukhala mwanawankhosa, iye ayenera kukhala wamphongo, woyamba kuchokera kwa mayi ake. Ameneyo anali Yesu, woyamba kuchokera kwa namwali Mariya. Ayenera kukhala wopanda chilema, ayenera kusungidwa ndikuyesedwa, kuti awone. Ndipo, oh, ndi mwangwiro bwanji momwe izo zinamufokozera Iye, Iye anali Mmodzi Wangwiro. Iye, mdani aliyense anachitira umboni kut Iye anali. Ngakhale Pilato anati, "Ine sindikupeza cholakwika mwa iye. Ndibweretsereni ine madzi ena."

57 Zindikirani, inu mukuyankhula za Iye! Ine ndikhoza kuyitana usikuuno ndikunena kuti, "Zekariya, kodi iwe ukuganiza chiyani za Iye?" Iye angakhoze kupereka chonena chake.

Ine ndikhoza ngakhale kumuyitana Eva, iye akhoza kunena kuti, "Iyo, Iyo inali Mbewu imene inalonjezedwa, mwa mkazi."

Ine ndikhoza kumuyitana Danieli, ndi kunena kuti, "Danieli, nanga bwanji iweyo? Ine ndimuika Iye pa mlandu ndi iwe."

Iye angati, "Iye ali Thanthwe limene linadulidwa kuchokera ku phiri."

"Iye ndiye amene Ine ndinati, 'Kwa inu Mwana wabadwa, Mwana wamwamuna wapatsidwa.'"

58 Ine ndikhoza kumuitana Ezekieli, ndi kunena kuti, "Kodi iwe ukuganiza chiyani za Iye?"

Anati, "Ine ndinamuwona Iye ngati mitambo, pansi pa mapazi Ake, akusuntha."

59 Ine ndikhoza kumuitana Yohane M'batizi, ndi kuti, "Kodi iwe ukuganiza chiyani za Iye?"

60 Iye angati, "Ine sindinkamudziwa nkomwe Iye, koma Iye amene anandiuza ine mu chipululu, anati, 'Pa Amene udzawone Mzimu ukutsikira ndi kudzakhalapo, Iye ndi Mmodzi yemwe ati adzabatize ndi Mzimu Woyera ndi Moto.'"

61 Ine ndikhoza kumuyitana Maria, ndikuti, "Maria, iwe ukuganiza chiyani za Iye?"

Maria angati, "Ine sindinamudziwe nkomwe mwamuna; koma Mzimu Woyera unandiphimba ine, ndipo anati, 'Chinthu icho chimene chidzabalidwe mwa iwe chidzatchedwa Mwana wa Mulungu.'"

62 Ine ndikhoza kunena osiyanasiyana awo. Ine ndikhoza kunena kwa Roma, "Inu mukuganiza chiyani?"

Inu mukuti, "Chabwino, abwenzi Ake adzachitira umboni. Nanga bwanji adani Ake?"

63 Tiyeni timuitane Pilato. Atatenga mbale ndikusamba mmanja mwake, ndi kuti, "Ine sindikupeza cholakwika chirichonse mwa Iye, koma mtengenipo Iye, kachiteni chirichonse chimene inu mukufuna," kuyesera kuti apeze kukonderedwa ndi ndale, iye anadzigwetsera yekha mu imfa kumtunda uko mu Norway, mu Sweden. Pamene, chaka chirichonse iwo amapita kumeneko kukawona madzi abuluu awo akutumphuka kachiwiri, ndipo nkumati ndi madzi amene iye anasamba mmanja ake kwa Khristu. Inu simungakhoze kumusamba Iye kuti achoke mmanja mwanu. Ayi, bwana, inu simungakhoze.

64 Ine ndinayang'ana pa kenturiyo wa Chiroma, "Kodi iwe ukuganiza chiyani za Iye? Ndiwe mmodzi wa adani Ake."

Iye anaika dzanja lake pamtima wake, ndipo anati, "Zoonadi ameneyo ndi Mwana wa Mulungu!"

Pilato anati, "Ine sindikupeza cholakwika mwa iye."

65 Poyamba, iye anali atayima pamenepo, moyipa kwambiri, oh, iye anali atakonzeka kutsutsa ndi chirichonse. Ine ndikumva kavalo akubwera, akuthamanga, akuthamanga kumatsika msewu. Apa pakubwera mmodzi wa alonda a mkachisi. Iye akulumpha kuchoka pa kavalo. Iye ali ndi kachidutswa kakang'ono ka pepala katapindidwa. Iye akuthamangira pamaso pa Pilato, ndipo akugwadira pansi, kumupatsa iye kachidutswa ka pepalako. Pilato wakale akutenga izo, inu mukudziwa. Ndipo unali molawirira mmawa umenewo, mokhala ngati, iye anali asanamwe khofi wake apobe. Iye anakwera pamwamba apo ndipo anayang'ana, iye anayamba kuyera, mawondo ake anayamba kugundana pamodzi. Tiyeni tiyang'ane pa phewa lake ndi kuwona lomwe liri vuto. Chimene chinalembedwa pa chidutswa cha pepala icho, mkazi wake wachikunja anati, "Usakhale kanthu kochita ndi Munthu Wolungama uyu, pakuti ine ndavutika ndi zinthu zochuluka mmaloto lero chifukwa cha Iye."

"Yudasi Iskarioti wakale, kodi iwe ukuganiza chiyani za Iye?"

Iye anati, "Ine ndapereka Magazi Osalakwa." Ndipo iye anatenga chingwe ndipo anali mwamuna wokwanira kuti adzipachike yekha. Anamuyesa Iye.

"Kodi inu mukuganiza chiyani za Iye, Mulungu?"

"Uyu ndiye Mwana Wanga wokondedwa, mvereni inu Iye!"

66 Anapitirizabe, palibe cholakwika mwa Iye. Ndithudi. Choyamba chochokera kwa mayi wokalamba, mayi nkhosa, mwanawankhosa anali. Yesu anali Mwana woyamba wa namwali, wobadwa mwa namwali. Ndithudi, Iye ankayenera kukhala namwali.

67 Taonani ichi, tsopano ine ndikufuna kuti inu muzindikire kachiwiri kuti gulu lonse liyenera kumupha iye, gulu lonse, ndi gulu lonse. Tsopano, ngati mungazindikire, penyani momwe izo zikuwerengekera, inu mukhoza kuwona kuti ndi chithunzithunzi. Tsopano penyani.

> *. . . tsiku la* fortini*. . . mwezi womwewo: ndipo gulu lonse la osonkhana a Israeli lidzamupha iye madzulo.*

68 Ndipo, inu muzindikira, Israeli yense anayima pamenepo ndipo anati, "Kutali naye iye! Mulole magazi ake akhale pa ife ndi pa ana athu." Iwo, kuchokera kwa Kayafa njira yonse mpaka mmusi, anachitira umboni imfa Yake. "Kutali naye iye! Tipatseni ife Baraba." Inu mukuzindikira izo? Ndipo Iye anafa pa firii koloko madzulo, "Iwo azayipha iyo madzulo." Ndi zokongola bwanji!

> *Ndipo iwo adzatenga. . . magazi, ndi kuwapaka iwo* pa. . . mphutu za chitseko ndi pamwamba*—mphutu ya* nyumba, *momwe iwo azidyeramo izo.*
>
> *Ndipo iwo adzadya nyamayo usiku, yowotcha pamoto,. . . mkate wopanda chotupitsa; ndipo ndi masamba owawa* iwo adza*dya izo.*

69 Ine ndikufuna kuti inu muzindikire tsopano. Mupirire nane.

> *Musadye* iyo osati *yaiwisi,* kapena yamphesa, kapena *yamadzi, koma yowotcha pamoto; mutu* wake. . . *miyendo* yake*, ndi kutumphuka kwake.*
>
> *Ndipo inu musalole kanthu ka iyo katsalire mpaka. . . mmawa; ndipo icho chimene* chatsalira. . . *chi*dzawotchedwa ndi moto.

70 Zindikirani, mokongola! "Tsopano, inu mutatha kupha mwanawankhosa, kugwira magazi ake, ndi kuwayika iwo pa nsonga ya chitseko, ndicho chidutswa cha apa, ndi pa mphuthu ya chitseko. Osati pakhomo, pansi; koma, pa mphuthu ndi pa feremu." Ngati mungazindikire izo, ndiwo Mtanda wangwiro. Oh, mai! Iye anati, "Ndipo pamene Ine ndiwona Magazi, Ine ndidzadutsa pa inu." Zindikirani, ndi tsiku lotani! Oh, mwamuna wochimwa, mkazi, mnyamata kapena mtsikana, mulole izi zilowerere mu mtima wanu wochimwa. Basi kusanafike Kudza kwa Khristu, ndi nthawi yoti ife tizilingalira, kudzifufuza tokha pa ifeeni, penyani.

71 Tsopano Iye anati, "Madzulo iyo inaphedwa." Mwanawankhosa anali pa zo-,. . . anabweretsedwa mkati mwa nyumba, atawotchedwa; mtundu wa mgonero, ndithudi. Tsopano Iye anati, "Mulowe mnyumba imeneyo ndipo musatulukenso, mpaka mmawa." Ameni! Kamodzi pansi pa Magazi, aleluya, khalani pamenepo! Ine ndikuyembekeza inu mukumvetsa zimenezo tsopano. Bwerani pansi! Mimbulu yolira ikhoza kubwera pamazenera.

72 Ine ndikukhoza kuwamva ena a iwo akubwera, ndi kuwona dona wamng'ono amene analowa mkati, ena a atsikana a ku Igupto, ndi kuti, "Marita, kodi iwe sukupita kovina usikuuno?"

"Ine ndiribe chikhumbo nkomwe." Pansi pa magazi, chinachake chinachitika!

73 Bambo anali wansembe wa nyumbayo, mmalo opatulika akale, nthawi yakale. Bamboyo nthawizonse anali wansembe, ndipo iye ankayenera kuti aziyang'anira banja lake. Ndi kusintha kotani lero, ana akumayang'anira bambo, mdziko lamakono. Koma bambo anayenera kuyang'anira nyumba yake. Iye ankapha mwanawankhosa, iye ankatenga udzu wamba, ndi kupaka iwo pazitseko, pa mphutu, ndipo icho chimakhala chitetezero chawo. Chabwino, iwo ankakhala mkati.

74 Ine ndikukhoza kuwawona ena onse akupita, akudyerekeza ndi kumapitiriza, kumati, "Tayang'anani pa gulu lija la otentheka! Oh, ndi magazi ankhosa akale pakhomo, kuyesera kunena chisokonezo ichi, 'chinachake chichitika.'" Koma izo zinatero! Chifukwa chiyani? Mulungu ananena chomwecho! Izo nthawizonse chimakhala choonadi pamene Mulungu anena chomwecho.

Ndi zimenezotu pamenepo, pansi pa magazi. Iwo analibe chikhumbo choti apite kunja. Ameni!

Inu mukuti, "Chikhumbo, M'bale Branham?" Uko nkulondola.

75 "Pakuti pali chotero tsopano," Aroma 8:1, "palibe kutsutsika kwa iwo amene abwera pakhomo." Ameni! Ine sindiri kudzichitira "ameni" ndekha, koma *ameni* amatanthauza "zikhale chomwecho"; ndipo ine ndikungomverera bwino kwambiri, ine ndimayenera kufuula "Ameni!" Taonani, analowa pakhomo! "Chotero palibe kutsutsidwa tsopano kwa iwo amene ali mwa Khristu Yesu, amene samayenda mwa thupi koma mwa Mzimu." Ndi zimenezotu pamenepo, mwa Khristu, amakhumba kuchita zimene Mzimu Woyera ukunena kuti achite. Sindikusamala zomwe dziko likuyenera kunena; palibe kutsutsika kwa iwo amene ali mwa Iye, akuyenda motsatira Mzimu.

Aisraeli amenewo onsewo anali mmenemo, okhutitsidwa. Ameni. Ndi ife apa, tayang'anani pa izo, ine ndikufuna kuti inu muziwone izo tsopano.

76 Patapita kanthawi apo panadzabwera mitambo, inayamba kuwuka, usiku waukali. Anthu anayamba kudabwa, "Kodi chikuchitika ndi chiyani kuno? Kukhala ngati kumverera kwachirendo."

77 M'bale, ngati panayamba pakhala kumverera kwachirendo pakati pa mafuko, ndi usikuuno! Chinachake chikukonzekera kuti chichitike. Aleluya! Ikadali nyimbo, "Pamene Ine ndiwona Magazi, Ine ndidzadutsa pa inu." Atate, kulibwino muyang'ane pa chitseko usikuuno, mufufuze. Tayani zitini zamowa zimenezo kuchokera mu firiji, mpukutu wa makadi umenewo kunja kwa chitseko, ndi kuitanira msonkhano wa pemphero mnyumba mwanu. Inu mukhoza kukhala dikoni, inu mukhoza kukhala trastii, inu mukhoza kukhala *ichi*, *icho*, kapena *chinacho*, koma, taonani, chimene ife tikusowa lero ndi chitsitsimutso cha kachitidwe-kachikale, chotumizidwa ndi Mulungu, chobadwa ndi Mzimu Woyera, kuliwongola fuko. Ndizo zoona.

78 Ife sitikusowa zafioloje, ndi zina zotero. Anthu mmipingo yawo, iwo akuyesetsa kupanga mipando yayikulu yabwino, ndi malimba aaakulu ndi zinthu, kumati, "Ndine wa gulu *ili*, ndine wa gulu *ilo*."

79 Ndine wokondwa usikuuno kunena, monga Paulo wakale, pamaso pa mfumu, "Munjira yomwe imatchedwa mpatuko, ndi yomwe ine ndimapembedzera Mulungu wa makolo athu." Aleluya! "Mpatuko, kupenga, kupusa," kwa dziko lapansi. Koma ulemelero kwa iwo amene ali mwa Khristu, ndi chimwemwe. "Wakufa," aleluya, inde, bwana, "obisidwa kutali mwa Khristu!"

Mukuti, "Chabwino, mdierekezi anabwera ndipo anadzanditenga ine." Ayi, iye sanatero! Inu munapita kwa iye.

80 Baibulo linati, "Ndinu akufa. Moyo wanu wabisidwa mwa Mulungu, kudzera mwa Khristu, wosindikizidwa ndi Mzimu Woyera." Mdierekezi angakhoze bwanji kukutengani inu? Inu munatuluka kunja. Ndiko kulondola, mdierekezi sanakupezeni inu. Zindikirani, zokongola!

81 Tiyeni tingopereka sewero laling'ono kwa ana. Ife tikufuna kuti iwo azigwire izi, nawonso. Tsopano penyani. Apa iwo ali mnyumbamo. Ndi pafupifupi ora la ziro limenelo. Zinthu zikuyamba kuchitika. Ine ndikuwawona iwo akuthamangira kunyumba kuchokera kovina. Iwo akulowa mkati. Iwo akubweretsa. . .pobwerera kunyumba, magalimoto akuthamanga kwambiri. Mphepo yolimba ikuwomba, iwo sakukhoza kudziwa komwe iyo ikuchokera, iyo ikuzungulira njira iyi ndi njira iyo.

82 Ngati kulibeko nthawi ngati imeneyo tsopano, ine sindikudziwa komwe iyo ili. Iwo sakudziwa choti achite, njira *iyi* ndi njira *iyo*.

83 Ndipo, chinthu choyamba inu mukudziwa, ine ndikumva kung'ung'udza kwakukulu ndi kubangula kukubwera kudutsa mdziko. Ine ndikuwona bambo wokalamba wansembe akuyenda chokwera ndi chotsika pansi, mwamphamvu basi monga iye akanakhoza kukhalira. Aleluya. Ine ndikumumva mnyamata wamng'ono akuti, "Abambo, ndine wamkulu mnyumba muno. Ine ndikuchita mantha."

"Usadandaule, mwana, magazi ali pa chitseko."

"Chabwino, nchiyani zonsezo . . . Ine sindinamvepo mphepo ikuwomba monga chomwecho, Adadi."

"Chimenecho ndi chiweruzo cha Mulungu."

84 Ndicho chimene ife talunjikako tsopano! Ife tinakana chifundo, ndipo palibe chimene chatsalira koma chiweruzo. Pamene iwe ukana chikondi cha Mulungu, palibe kanthu kamatsalira kwa iwe koma chiweruzo. Ndiko kulondola, mphepo yolira paliponse! "Kodi zonsezi ndi zachiyani, kusokonezeka kwa nthawi, kupsyinjika pakati pa mafuko?" Chiweruzo! Eya, inu mukhoza kuyika a—khalidwe labwino mu chigawo chirichonse, ndipo inu nkusakhozabe kuziletsa izo. Amuna, iwo akupita kokamwa, akazi akupita kosuta ndudu, inu mukupita kukapitirira ku ziwonetsero zanu, inu mukhoza kumapitirira monga inu munkachitira nthawizonse, basi monga nkhumba ku matope ake ndi galu ku masanzi ake, osamulemekezanso Mulungu kuposa kanthu kalikonse mdziko. Ndipo anthu amene akuyesetsa kuti azikhala moyo woyenera, inu mukumawatcha iwo oyera-odzigudubuza ndi otentheka, ndi china chirichonse, osadziwa kuti solo yanu yomwe yayesedwa pamiyeso ndipo sikuyembekezera kalikonse koma chiweruzo. Inde, bwana.

Ine ndikukhoza kukawona kamunthu kakang'onoko kakuti, "Adadi, tulukani panja ndipo mukayang'ane, ndipo mutsimikizire kuti magaziwo ali pamenepo."

85 Ine ndikukhoza kumuwona mnyamata wamng'ono ndi mtsikana akugwirana manja, ndi kupita pazenera, ndikuti, "Adadi, bwerani kuno! Taonani apa!" Ine ndikuwona, akubwera kudutsa Igupto, mapiko awiri aakulu akuda akupindira mmbuyo ndi mtsogolo. Ndi chiyani chimenecho? Imfa. Ine ndikuwona iwo akuthamangira pansi monga *chonchi*, ine ndikumva kufuula kukubwera kuchokera mnyumba. Panalibe magazi pamenepo, imfa inakantha banjalo. Kulekanitsidwa!

86 Iyo ikudutsa usikuuno, aponso, m'bale. Osati mwathupi; mwauzimu. Pamene iwo ankatsogolera zachirengedwe, Iye akutsogolera zauzimu lero. Icho chinali chitsanzo, mthunzi.

87 Ine ndikuziwona izo kutaliko, ndipo ndikuwamva akazi akuthamanga, akufuula, ndipo banja lonse monga choncho. Mwana wamwamuna wamkulu anali atafa.

Ine ndikukhoza kuwamva abambo aang'ono akupita. . . mwana wamng'ono akupita kukawagwedeza abambo ake, kuti, "Adadi, Adadi, pitani mukayang'anenso! Mukatsimikizire!"

Ine ndikukhoza kuwawona abambo achikulire akubwerera ku chitseko, ndipo akuti, "Inde, mwana, iwo alipo."

"Inu mukutsimikizadi kuti ndife otetezedwa, Adadi?"

"Inde, bwana!"

"Inu mukudziwa bwanji?"

"Mulungu anati, 'Pamene Ine ndiwona magazi, Ine ndidzadutsa pa inu.'" Ndiko kulondola, kuyang'anira magazi.

88 Apa pakubwera angelo, akudzasuntha kachiwiri. Ine ndikuwawona iwo akusunthira mmwamba, akukhota kuchoka pa malo kupita pa malo. Ndikuwawona iwo akudzatsikira panyumba, kenako akudzabwereranso, "Ine ndawona magazi."

Apa iye akubwera kunyumba iyi, ine ndikumuwona iye akubwera, ndipo mwana wamng'onoyo akuti, "Oh, Adadi, inu mukutsimikizadi?"

"Ndife otsimikiza mwangwiro, mwana."

89 Ndipo mngeloyo akutsikira pakhomo, akudzatambasula mapiko ake aakulu kuti alowe mkati, iye akuwona magazi ndipo akuwuluka kumapita. Aleluya! Vuto ndi chiyani? Iye wawona magazi.

90 Pambuyo pake, mverani apa, "Ndipo inu mudzadya ndi kulola. . ." Mphindi yokha tsopano mpaka ine ndiwongole izi, tsopano, pamene ine ndikufuna kuti ndiwerenge. Ndife pomwe apa, "Ndipo inu musalole kanthu katsalire kufikira mmawa." Tsopano zindikirani ndime ya 11.

> *Ndipo potero inu mudzadya iwo; mutadzimangira mchiuno mwanu, nsapato zanu pamapazi anu,. . . ndodo yanu mdzanja lanu;. . .*(M'bale, inu mwakonzeka!)

91 Tiyeni titembenuzire pakali pano ku Aefeso, mutu wa 6, mphindi chabe, ndi kuwerenga pang'ono pokha apa za momwe ife tiyenera kuvalira, nafenso, pafupifupi nthawi imeneyo. Chabwino, Aefeso 6:12, inu amene mukuzilemba izo.

> *Pakuti ife sitilimbana nawo mwazi ndi thupi, koma timalimbana ndi maukulu, motsutsa mphamvu, motsutsa. . .olamulira a. . .mdima wa dziko lino, motsutsa mizimu yoyipa mmalo ammwamba.*

92 Mukuona komwe kuli nkhondo yathu lero? Mukuona chimene mngelo wa imfa ali? Ndi mphamvu yauzimu, kuipa mmalo ammwamba mwamba, malo aakulu, malo aakulu.

> *Chifukwa chake tengerani kwa inu zida zonse za Mulungu, kuti inu mudzakhoze kupirira* a—*tsiku loyipa, ndipo mutachita zonse, kuti muyime.*

Imani! *Imani chotero, mutadzimangirira mchiuno mwanu pa* inu, *ndi choonadi,* . . .

93 Ine ndingomenya pamenepo, chifukwa ine ndikufuna kubwerera ku phunziro langa. Mpenyeni iye, iye akupita patsogolo, ndipo akuti, "chapachifuwa, ndi chisoti," ndi china chirichonse. Ndikulakalaka ife tikanamuveka msilikari ameneyo kwa inu pano, koma ife tiribe nthawi.

94 Tiyeni tingotenga chiwuno, "atadzimangirira ndi lamba," uyo ndi—uyo ndi lamba yemwe amagwirizira zina zonse pamodzi. "Muzimange mchiuno mwanu ndi Choonadi." Mu tsiku, m'bale, pamene pali mitundu yonse ya malingaliro ndi kutentheka, ndi nthawi yoti mudzimange nokha mchiuno ndi Choonadi. Aleluya! Yesu anati, "Ine ndine Choonadi." Choonadi!

95 Ine ndikukuuzani inu, pamene anthu akuti, "Nanga bwanji *izi*? Nanga bwanji *izo*?" Ndi zabwino kuwona Choonadi chakale icho chitakumangirirani inu, (sichoncho izo?) kudziwa pamene iwe waima. Ndiye imani pamenepo! Asiyeni iwo aziti, "Chabwino, inu muli ndi *ichi*, *icho*, ndi *chinacho*." Inu mukudziwa pamene inu mwaima. Mukhale ndi Zida zonse mutazimangirira, ndipo ndi—mchiuno chozungulira *apa*, chomangidwa bwino komanso cholimba, ndi kukokera pansi ndi Choonadi cha Mawu a Mulungu chozikika mu mtima mwanu.

96 Adierekezi onse ku gehena sangakhoze kukukhumudwitsani inu. Uko nkulondola. Inu mukhoza kukumana ndi Satana, ndikuti, "Kwalembedwa." Aleluya!

"Oh, ine ndikuwuzani inu, m'bale, kodi inu munatenga njoka?"

"Ayi, bwana. Ine ndimakhulupirira Yesu Khristu."

"Kodi inu munachita *izi*, *izo*, kapena *zinazo*?"

"Ayi, bwana. Ine ndinalandira ubatizo wa Mzimu Woyera." Atamangira mozungulira, chida, atamangirira mchiuno Choonadi!

97 Tsopano, iwo anali atakonzeka pamene iwo anali akudya. Mulungu akufuna kuti inu muvale inu musanadye mgonero uwu. Ndipo, m'bale, inu musanati mudye iwo molondola, inu muyenera kuti muvale. Pakuti, Mzimu Woyera umene uli mu mtima mwanu, udzabweretsa Mzimu Woyera, miyoyo pa Mawu a Mulungu.

98 Inu mukudziwa lomwe liri vuto ndi mpingo lero, abale? Ine ndikukhulupirira kuti mpingo uli mu chikhalidwe cha kuchepa kwa magazi m'thupi—Magazi atuluka mwa iwo. Mwachitsanzo, bwanji ngati ine ndikanakhala dokotala, ndipo munthu wamkulu kwambiri, wamtali mapazi sikisi, nkubwerapo, ndipo iye nkudzati, "Kuti, dokotala, ine—ine—ine

ndine wofooka kwambiri, ine ndikulephera kudzuka. Ine—ine ndikungozandima pamenepo"?

Ine ndingati, "Chavuta ndi chiyani?"

"Chabwino, ine sindikudziwa. Basi ine ndafooka kwambiri."

Ine ndingati, "Chabwino, tsopano, kodi zinthu zina za mthupi . . .?"

"Inde, izo ziri bwino."

Ndipo ine ndingati, "Chabwino, kodi inu munadya liti komaliza?"

"Chabwino . . . "

"Iwe uli pafupi munthu wa mapaundi handiredi ndi eyite."

"Ine ndinadya chitumbuwa cha theka, dzana."

99 Ine ndingati, "Bambo, iwe ukungofa ndi njala! Pita ukadye chakudya chabwino chokwanira, ndipo iwe sufooka kwambiri chomwecho."

100 Ndipo ndiro lomwe liri vuto ndi mpingo lero. Ndife ochuluka mu chiwerengero, koma, m'bale, ife tikufa ndi njala! Aleluya! Inu mukuchita mantha kuti woyandikana naye wanu ayankhula chinachake. Chimene ife tikusowa ndi kugwedezeka kwabwino kwachikale, kwa Mzimu Woyera. Aleluya! Manja onse mmwamba mu mlengalenga, ndikuti, "Ambuye, ndidyetseni ine!" Utadzimangirira ndi zida, ukuguba chitsogolo.

101 Zodabwitsa zinali zitachitika. Mu ndime ya 38 ife tikuwerenga izi.

> *Ndipo gulu losakanikirana* nalonso linapita kumeneko *ndi iwo; ndi nkhosa, ndi gulu,* . . . la *ng'ombe.*

102 M'bale, gulu losakanikirana! Zodabwitsa zinali zitachitika, chitsitsimutso chachikulu chinali chikuchitika. Anthu anali akupulumutsidwa, akubwera mkati. Ndipo gulu linapita kumeneko, kukatsanzira zimenezo, iwo anapita kumeneko, kumakachita ngati kuti iwo anali okhulupirira. Ndithudi, iwo anavala nsapato zawo ndi chirichonse, ndipo anakhala okonzeka. Koma gulu lomwelo losanganikirana lomwe linadya mgonero, ndipo linapita pa kugubako, linali lomwelo limene linayamba kung'ung'udza ndi kuwapangitsa ana (apa mtima) a Israeli, mitima yawo, kuti itembenukire ku Igupto aponso. Ndi zomwe ziripo usikuuno, m'bale. Kukhala ndi chitsitsimutso, ndipo padzakhala gulu losakanizikana, ndithudi monga chirichonse. Ena a iwo adzayesa kubwera mmenemo, kudzatsanzira. Pamene inu mukuyankhula za kukonzedweratu . . .

Winawake anandiyimbira ine tsiku lina, anati, "Nanga bwanji zimenezo ndiye, ngati Mulungu anakonzeratu?"

Ine ndinati, "Ingowerengani Aroma, mutu wa 8, ndi wa 9, ndipo inu mumvetsa." Ndipo ine ndinati, "Mulungu amachitira chifundo Iye amene wamchitira chifundo."

"Ndi cha ntchito yanji kulalikira ndiye?"

Ine ndinati, "Imeneyo ndi ntchito ya inu ndi ine, monga atumiki."

103 Yesu anati, "Ufumu wa Mulungu uli ngati munthu amene anapita kunyanja ali ndi khoka mdzanja lake. Iye anaponyera khoka kumeneko, mmenemo, iye analikokera ilo mkati. Umenewo unali Uthenga. Mmenemo iwo anali ndi akamba, mbozi za mmadzi, njoka, achule obiriwira, njoka, china chirichonse. Ndipo iye anali ndi nsomba mmenemo! Aleluya!

104 Chinthu choyambirira inu mukudziwa, pamene chitsitsimutso chinatha, ndipo ukonde wa Uthenga utachokapo, kamba wakale anati, "Ine ndimadziwa kuti panalibe kanthu kwa Iwo." Mbozi yakale yammadzi inati, "Ine ndikuzikhulupirira izo, inenso," kubwereranso ku . . . nkhumba, ku matope ake kumene. Serpenti inati, "Ine sindimawukhulupirira Iwo, kuyamba ndi kuyamba."

105 Koma kuli nsomba zina kumeneko! Aleluya! Aleluya! Yakwana nthawi yoti azitumiki aponyere ukonde wa Uthenga, awukokere iwo mkati. Mulungu amadziwa imene ili nsomba. Iye anali kamba, kuyamba ndi kuyamba; ndipo iye anali nsomba, kuyamba ndi kuyamba. Mulungu akudziwa chimene chiri, ine sindimadziwa. Ndi ntchito yanga kuponyera ukonde mu mtsinje, kuwakokera iwo mmwamba, ndikuti, "Ndi awa apa, Ambuye." Aleluya! Ameni. Ndithudi, ndi zimenezo, ndiwo ukonde wa Uthenga.

106 Inu mukudziwa tsiku la lero. Ine ndinapita kuno osati kale litali ku malo, iwo anati, "Ife tikhala ndi mgonero." Ndipo iwo anatenga chidutswa chakale cha mkate, ndipo anawudula iwo monga *chonchi*, mzidutswa, ndipo anapereka iwo pakati pa gulu la anthu kumeneko, ndipo aliyense mu mpingo anadya mgonero. M'bale, zimenezo si zoona. Mtima wako uyenera kukhala pachiyanjano ndi Mulungu iwe usanadye mgonero.

107 Yesaya analosera za zimenezo, mutu wa 28 ndi ndime ya 8, ngati inu mukufuna kuti muziyang'ane izo. Iye anati, "Magome adzaza masanzi, zanyansi zonse ndi zauve paliponse." Iye anati, "Ndi ndani yemwe ine ndingakhoze kumuphunzitsa Chiphunzitso? Ndani yemwe ine ndingakhoze kumupatsa kumvetsa? Iwo amene achotsedwa ku bere!" Ana athu aang'ono kumbuyo kuno kumangosewera pamenepo, pamene ife timayenera kuti tizimuphunzitsa winawake mphamvu za Mulungu, ife tikukanganabe ngati ziri zolondola kuti tichite *izi* kapena *izo*. "Magome adzaza ndi masanzi!"

Ine sindingakhoze kuyimira pamenepo. Tiyeni tipitirire, ine ndiyenera kufika pamalowo. Chabwino.

108 Iwo anali atavala zida zawo, malamba awo, iwo ankaguba akutuluka. Iwo anabwera molunjika kumene ku Nyanja Yofiira. Farao anasangalala kuwalola iwo kuti apite. Ndipo pamene iwo anadzafika ku Nyanja Yofiira, pamenepo iwo anawona ankhondo ake akubwera, akuwalondola iwo. Ndipo pamenepo iwo anali, anamanga misasa apo pomwe, mapiri ndi zipululu ku mbali *iyi*, ankhondo a Farao akubwera njira *iyi*, Nyanja Yofiira patsogolo pawo. Koma njira ya Mulungu inadutsa pa Nyanja Yofiira. Malingana ngati ndikudziwa kuti njira Yake ikutsogolera, ndizo zonse zimene ine ndimazisamalira, mozingopitirira kumayendabe. Anati, "Mose," Aleluya, "tenga ndodo imeneyo, ziyenda uzipita cha ku madzi amenewo." Ameni!

"Ndi chiyani chiti chichitike, Ambuye?"

"Imeneyo si ntchito yanu. Uzingopitirira kumayenda!" Ameni.

109 Kazilalikirani Uthenga, Tom Merideth ndi ena nonse a inu anyamata. "Kodi chichitike ndi chiyani?" Si ntchito yanu; muzingolalikira basi! Muzipereka matamando kwa Mulungu.

110 Apa iwo akupita, akusunthira kumusi uko. Mmodzi mwa olembawo ananena kuti Mulungu anali mu Lawi la Moto lija, "Ndipo Iye anayang'ana pansi ndi maso okwiya." Ndipo anati, "Pamene Iye anatero, Nyanja Yofiira inachita mantha ndipo inayamba kubwerera mmbuyo, ndipo Israeli anadutsa pa nthaka yowuma." Sanadetse ngakhale mapazi awo ndi matope.

111 Chabwino, anyamata awa anabwera, anati, "Ndife anthu basi monga iwo aliri, ndipo ife timapembedza chimodzimodzi monga iwo amachitira, kotero ife tichita zimenezo." Ndipo pamene iwo anakafika kumeneko, iwo anapeza kuti iwo sakanakhoza kukwanitsa izo.

112 Ndipo ndicho chimene chiti chidzachitike limodzi la masiku awa, m'bale, pamene nthawi yolekanitsa idzafika. Ndipo kwa inu, iwe membala wofunda wa mpingo, amene ukuyesetsa kuti utsanzire Chikhristu, limodzi la masiku awa inu mudzayesa kutsatira gulu la Mzimu Woyera lija, ndipo inu mudzapeza kuti magudumu anu adzagulukira kutali mmatope kwinakwake. Uko nkulondola. Panali anamwali teni anapita kukakumana ndi Ambuye, faivi a iwo anali ochenjera, ndi faivi opusa. Ikani Mafuta mu nyali yanu, ikonzeni iziwala, limodzi la masiku awa iwo adzapita mmwamba. Ndipo kunali kulira ndi kusisima, ndi kukukuta kwa mano!

113 Ndipo Aigupto osadulidwa aja, bwanji iwo sanathe kukwanitsa zimenezo? Iwo anali osadulidwa. Iwo sanali mu pangano. Ngati iwo akanakhala okhulupirira odulidwa, Mulungu akanayenera kuti awazindikire iwo mofanana monga Iye anamuzindikira Israeli. Ulemelero! Oh, ine ndikanakonda ndikanakhala pawiri usinkhu wanga pakali pano. Ine ndikumverera mwachipembedzo, ine ndithudi

ndikutero. Zindikirani, iwo anali osadulidwa. Iwo sanali mu pangano, ngakhale iwo anali amuna. Iwo anali atavala bwino basi, ndi bwinoko. Iwo ankakhala mwabwino basi. Iwo anali ndi nyumba zabwinoko. Iwo anali mu gulu labwinoko la anthu, kuganiza mwachidziko. Iwo ankapita ku tchalitchi chimodzimodzi ndi mmene ena onse ankachitira. Iwo anali atatsatira nthawi yonseyo. Musandiuze ine kuti iwo samadziwa chirichonse chokhudza Mulungu. Yosefe anali atawauza kale ndipo anafalitsa nkhani kumusi kumeneko, zaka foro handiredi mmbuyomo. Zedi, iwo anatero. Koma iwo anaganiza, "Gulu la otentheka ilo, ife tikhoza kuchita chirichonse chimene iwo angakhoze." Koma iwo analephera. Mulungu anazindikira mdulidwe wokha. Apo iwo anapita.

114 Nzosadabwitsa Davide wamng'ono wakale anaima, anati, "Inu mukutanthauza kundiuza ine kuti magulu ankhondo a Mulungu wamoyo angaime pano, nkumusiya Mfilisti wosadulidwa ameneyo anyoze makamu a Mulungu wamoyo?" Iye anati, "Ndiyikeni ine pa chinachake, ndiloleni ine ndipiteko." Inde, bwana. Tipatseni ife a David ena.

115 Pamene iwo anadzawoloka mtsinjewo, atafika kutsidya linalo. Mulungu anangotsekera izo mkati, apo panali ogwiritsa ntchito akalewo. Kodi inu mungakhoze kulingalira momwe Ayuda aja anamverera? Anayang'ana kumbuyo uko, ndipo apo panali chinthu chomwecho chimene chinkapanga, ndi kuwakwapula iwo, ndi kumawamenya pa nsana pawo kukhala polezeka, ndi kumawakokera iwo uko monga *chonchi*, anali atafa, akuyandama mu nyanja.

116 M'bale, pamene iwe udutsa Nyanja Yofiira ya Magazi a Yesu Khristu, chizolowezi chirichonse chakale chonyansa chimene chinakupititsa iwe ku zinthu zimene iwe sukanakhoza kuzichita, iwe udzazipeza izo zitafa mu Magazi a Yesu Khristu, (aleluya, uko nkulondola), zikuyandama kumusi kwa mtsinjewo.

117 Nzosadabwitsa Mose analowa mu Mzimu! Tsopano, inu mukunena za ife kukhala ndi mtundu wina wa chipembedzo chatsopano, yang'anani pa izi. Miriamu, mneneri wamkazi, iye anayang'ana kunja uko, iye anatenga nkhotcho, ndipo iye anayamba kumenya ndi kumavina, ndipo iye anatsikira mmphepete mwa nyanja, akuvina, akumenya nkhotcho iyi. Ndipo ana aakazi a Israeli anamtsatira iye, akuvina, ndi kumayimba, ndipo akumenya nkhotcho iyi. Ndipo Mose anakweza mmwamba manja ake, ndipo anatengeka kwambiri mu Mzimu Woyera mpaka iye anayimba mu Mzimu. Aleluya! Uko nkulondola. Uko nkulondola.

118 Mzimu Woyera womwewo, umene unali pa Mose, uli mnyumba ino usikuuno. Aleluya! Mmodzi yemweyo yemwe anamupangitsa Miriamu kuvina, ali pano usikuuno. Mulungu ndi Mulungu, ndipo samasintha. Inde, bwana.

Ndiye inu mukuti, “Tayang’anani pa gulu ilo la otentheka.”

119 Koma panalibe aliyense amene anasekedwa pamenepo, iwo onse anali atapita. Iwo anali nazo zonsezo kwa iwoeni. Oh, izo zidzakhala ulemelero posachedwapa! Tinali ndi nthawi yopambana. Tayang’anani pa iwo. Tiyeni tiwawone iwo kwa mphindi zingapo tsopano, ngati ife tingawafikitse iwo ku “Thanthwe” mu maminiti angapo otsatirawa, ngati ife tingakhoze kutero. Ine ndachedwa tsopano, mundikhululukire ine. Koma ine ndikungomverera bwino kwambiri, ine sindingakhoze kusiya pakali pano, kotero dikirani miniti yokha, ngati inu mungathe. Tiyeni tiyang’ane pa iwo pang’ono pokha. Oh, ine ndimakonda kuwayang’ana iwo.

120 Nyimbo yayikuluyo itatha, ndi kufuula kwakukulu, ndi kukhala ndi aleluya, nthawi yopambana, iwo anayamba kudutsa mchipululu, ndipo anawatsogolera iwo molunjika kumene ku madzi owawa. Kodi izo sizodabwitsa? Oh, mai! Mpaka kukalowa mu yesero, mpaka kumene madzi anali owawa ndipo iwo sankakhoza kumwa. Iwo analibe kanthu koti adye. Panalibe choti adye, ndipo madzi anali owawa. Ndipo, taonani, mtsinje umenewo wa *Marah*, “madzi owawa,” atayikidwa mu njira ya Mulungu, Iye anali kuwatsogolera ana Ake. Kodi izo si zachirendo? Zimawoneka ngati Mulungu akanazilambalala izo, koma Iye anawatsogolera iwo molunjika kumene ku madzi amenewo.

121 “Ena kudutsa mmadzi, ena kudutsa mnamondwe, ena kudutsa mmayesero akuya, koma onse kudzera m’Magazi.” Ndiyo njira ya Mulungu yowatsogolera anthu Ake.

122 Inde, ataimirira pamenepo, “Kodi ife tichite chiyani?” Aleluya! “Ife tawatsatira Ambuye. Ife tabwera kudutsa m’magazi. Ife tadzilekanitsa tokha.”

123 Mose anati, “Imani njii!” Ndiko kulondola. Ndipo mu mayesero lirilonse Iye adzapanga njira yopulumukirapo. Panali chitsamba chaching’ono chitayima pambali pamenepo. Aleluya! Iye anadula chitsamba chimenecho ndipo anachiponyera icho mmadzi, ndipo madzi amenewo anakhala okoma, akutumphuka, okondwa. Ndi nthawi inanso yofuula yomwe iwo anali nayo! Ameni.

124 Nthawi yomweyo mdierekezi akutsekereza iwe pakona, akuti, “Ine ndamupezeketsa iye pompano. Mnyamata, iye sangakhoze kusuntha tsopano. Ine ndamupezeketsa iye pompano.” Ndiye Ambuye adzabwera, ndipo Mtanda udzagwera patsogolo pathu pomwe, ndipo (aleluya) kutali ife tidzapita. Dokotala akati, “Palibe chomwe chingachitike kwa iwe.” Oh, mai! Oh, wina akati, “Iwe ukudziwa, iwe ukupenga, iwe uchita musala,” kapena chinachake chonga zimenezo, ndiye Mulungu adzabwera, kudzatsanulira mdalitso pa iwe. Ingoiwala za zimenezo. Mulungu amadziwa kumene Iye akutsogolera.

Ameni. Psyii! Ine ndikukhala ndi nthawi yovuta pano, ine ndikukuuzani.

Zindikirani, iwo analibe chirichonse choti adye. Mulu wawung'ono wa mkate umene iwo anali nawo, iwo anali atawudya kale iwo. "Kodi ife tichita chiyani tsopano?"

Anati, "Nonse inu pitani mukagone, ndipo mukasale usikuuno." Kodi inu munayamba mwayeserapo zimenezo? Zimakhala bwino nthawizina.

125 Ndipo mmawa wotsatira, iwo anatuluka kunja, ndipo apo panali timitanda tating'ono ta mkate titagwera pansi ponse. Mulungu anali atavumbitsa mkate kuchokera Kumwamba. Chabwino, iwo anatola izo ndi kuyamba kulawa izo. Bwanji, akuti, "Izo zikukoma ngati uchi ndi mkate wophika." Oh, mai! Zikuchita chiyani? "Zikukoma ngati uchi." Iwo anayamba kudya izo. Anati, "Bwanji, izo ndi zabwino." Ndipo iwo anangoyamba kusonkhanitsa ndi kumadya, pakuti ndani akanati asakhale nazo izo. Kukoma ngati uchi mu Thanthwe!

126 Inu mukudziwa, ine nthawizonse ndimanena Davide, ndi nkhosa yaing'ono iyo. . . legeni ya m'busa kapena chikwama, chikwama chomwe iye anali nacho, iye nthawizonse ankanyamula uchi mmenemo, inu mukudziwa. Ndipo nthawi iliyonse ina mwa nkhosa zake ikadwala, iye amatulutsa uchi m'menemo ndipo amaupaka—kupaka pa mwala wa laimu, umene unali machiritso akale. Ndipo chinthu choyamba inu mukudziwa, nkhosa zimakhoza kufika pamwamba apo ndi kupita kukanyambita pa thanthwe limenelo. Ndipo pamene iwo anyambita pa thanthwe limenelo, iwo ankanyambitapo uchi, iwo ankanyambita mwala wa laimu ndi kumachiritsidwa. Kodi izo sizodabwitsa?

127 Bwanji, ine ndiri ndi chikwama chonse chodzaza ndi uchi pano usikuuno, ndipo ine ndichiyika icho pa Thanthwe, Khristu Yesu, ndipo inu nonse ana ankhosa mupite mukanyambite pa Thanthwe limenelo, "kunyambita, kunyambita, kunyambita" ndipo umakhala wotsimikiza kuti utulukamo mmenemo. Aleluya! Inde, bwana. Oh, inde, bwana. [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi].

128 Kuti akhalapo utali wa nthawi yonse imene ali paulendo! Ndipo iwo amatha, iwo samasiya nkomwe! Tsopano, iwo anali oti azisonkhanitsa okwanira usiku uliwonse kuti akhalepo mpaka usiku wotsatira. Ngati iwo anasiya chirichonse, kuti, "Tsopano tisonkhanitsa ochuluka kwambiri usikuuno, sitidzabwerera ku chitsitsimutso mawa usiku. Ife tingosonkhanitsira mmenemo ochuluka onse usikuuno, ndiyeno mawa usiku tidzakhala nawo ochuluka otsalira kwathu." Ayi, ayi, izo zimakhala ndi mbululu mmenemo. Inde, bwana.

129 Ndiro lomwe liri vuto ndi zokuchitika za anthu ambiri. Inu mukuti, "Chabwino, m'bale, ine ndinkakhala ndi chisangalalo."

Inu mwayesera kusunga chinachake. M'bale, zomwe ine ndinali nazo usiku watha zapita. Zomwe ine ndiri nazo tsopano! Aleluya! Ameni. Zowachitikira anthu ena ziri ngati chitsime chong'aluka, inu mukudziwa. Uko nkulondola. Tiyeni tizitenga nyama yatsopano usiku uliwonse, tizipanga sitepe yatsopano usiku uliwonse. Ndipo izo zinkaimira. Ndizo ndendende choonadi, m'bale. Uko nkulondola. Chimene ife tikusowa ndi Mzimu Woyera wachikale. . .

130 Oh, ife tiri nawo matchalitchi ambiri, oh, mai, mamembala abwino. Oh, ndalama zochuluka mmatchalitchi masiku ano, zedi, zochuluka momwe inu mukufunira, zoti muziyendetsera nazo tchalitchi. Ife tiri nazo zonse izo, koma ife tiribe Moto.

131 Kodi inu mungalingalire kupita kumusi kuno ku kagwira ntchito zamagalimoto ndi kumanga mndandanda wabwino waukulu cha sitima apa, ndi kupeza munthu wophunzira wabwino yemwe amadziwa kuyendetsa izo, kumukhazika iye pansi pa mpando wapamwamba, ndipo anthu onse ali mkati, nkuti, "Chabwino, tiyeni ife tizipita." Ndipo kukankha, kukankha, palibe choti chipite. Iye anafika, nkuti, "Kulibwino ndikokere muluzu." Iye alibe ngakhale nthunzi yokwanira yoimbira muluzu. Ndiko kulondola.

132 Anthu ambiri alibe ngakhale nthunzi yokwanira kuti anene "Ameni." Inu mukhoza kukhala nazo mwaulere. Oh, aleluya! Chimene ife tikusowa usikuuno! Mvetserani, chitukuko chimabwera ndi moto, bwererani ndipo mukapeze mafuko omwe amagwiritsa ntchito moto; moto umapanga zovala zanga, moto umapanga kuwala, moto umaphika chakudya changa, chirichonse chimabwera ndi moto. Ngati inu mukukhala mu chitukuko chamakono, inu mumakhala ndi moto. Ngati inu mukukhala mu Kukhalapo Kwauzimu kwa Mulungu, inu mumabatizidwa ndi Mzimu Woyera ndi Moto. Aleluya! Kulondola.

133 Iwo anaponyera nthunzi ina mmenemo, m'bale, chim'phika chakale chaching'ono, kuphika ndi kuphulika, ndi kulumpha ndi kutumphuka. Chinthu choyambirira inu mukudziwa, inu mumakoka kherere, ndipo kutali kumusi kwa kanjira iye amapita. Uko nkulondola. Izo ndi zomwe ife timazisowa.

134 Zikundikumbutsa ine nthawi ina, m'bale ndi ine tinali kuno ku Lancassange Creek, ndipo ife tinali kuyenda pamenepo, ife tinali ndi kamba wakale. Ndipo icho chinali chinthu chowoneka-moseketsa kwambiri, iye amakhoza kuponya mapazi amenewo pamene iye ankayenda.

135 Ine ndinamutenga mtsikana wanga wamng'ono awiri a iwo, tsiku lina, pafupi wamkulu *chomwecho*. Ine ndinali nditaima pamenepo lero ndikuwayang'ana ana aang'ono amenewo, ndipo ndimaseka. Iye amayesa kusisita mutu wake ndi phazi lake monga *choncho*. Ine ndinali kuyang'ana pa iye. Ndipo

mwamsanga pamene iwe umukhudza iye, kapena chinachake, iye amapita “sshuu,” kubwereranso mu chigoba.

136 Umo ndi momwe zimakhalira ndi zina za chipembedzo chozizira chakale chomwe inu muli nacho lero. “Ine sindidzabwereranso ku chitsitsimutso chimenecho,” sshuu! “Ine ndine wa Presbateria, Methodisti, Lutheran, ine ndine wa *ichi*. Aleluya. Iye sanagwirizane ndi ine, ine—ine ndabwerera mu chigoba.” Pitirizani. Oh, chipembedzo chakale chotsekeredwa mkati chimenecho, cha kamba.

137 Ine ndinati, “Ine ndimukonza iye,” ndipo ine ndinamutengera iye ku mtsinje. Poyamba, ine ndinapeza ndodo, ine ndinayesa kumumenya iye, izo sizinachite ubwino uliwonse. Basi sizinachite ubwino pang’ono, iye anangogona pamenepo. Ndipo ine ndinangomukwapula iye mwamphamvu monga ine ndikanathera, iye anangogona pamenepo. (Inu simungakhoze kuwumenyera Iwo kulowa mwa iwo, osati mpang’ono pomwe. Ayi, palibe chifukwa choyesera izo, kuwawopsyeza iwo, ndi chirichonse.) Ndipo ine ndinamutulutsa iye kunja, ine ndinati, “Ine ndimukonza iye,” Ine ndinamuponyera iye pansi mmadzi. Mathovu pang’ono okha anatulukira, iye anangokhala mwanjira yomweyo.

138 Chabwino, inu mukhoza kuwakonkha iwo, kuwatsanulira iwo, chammbuyo, kutsogolo, chirichonse chimene inu mukufuna. Iwo akalowa mmenemo, wochimwa wowuma; ndi kutulukamo, wonyowa. Ndizo zonse, wochimwabe!

139 Inu mukudziwa momwe ine ndinamupangitsa iye kuti asunthe? Ine ndinapita ndikukatenga nkhuni zodzaza dzanja ndikuyatsa moto waung’ono ndikumukhazika mnyamata wokalambayo pamenepo. Iye anasuntha pamenepo, m’bale.

140 Ine ndikukuuzani inu, chimene mpingo ukusowa lero ndi Moto wanthawi zakale, wa Mzimu Woyera woyaka pansi pawo. Ulemelero kwa Mulungu! Ndicho chimene ife timachisowa. Moto udzasuntha mpingo, ndipo palibe chinanso. Ndiko kulondola. Inde, bwana.

141 Chabwino, icho chinali choyimira, choyimira chokongola. Inde, bwana. Izo zinkaimira chinachake, pamene mana amenewo ankagwa, izo zinkatanthauza . . . Mulungu anawapatsa iwo atawoloka Nyanja Yofiira (choyimira cha Magazi), ndipo ogwiritsa ntchito anafa. Mulungu anayenera kuchirikiza moyo wawo. Ndipo Iye ankayenera kuwapatsa iwo chinachake, pokhala kuti iwo anali atadzilekanitsa okha ku dziko la kwawo, ndipo iwo anali uko mu chipululu. Iwo anali amwendamnjira kumeneko. Iwo anali paulendo, ndipo Mulungu anayenera kuchirikiza moyo wawo, kotero Iye analonjeza kuti Iye adzawapatsa chirichonse iwo anali kuchifuna. Kotero Iye anachita zimenezo, ndipo Iye anavumbitsa mana pansi. Chinali choyimira chokongola!

142 Pa Tsiku la Pentekoste pamene Mpingo uwu unakhazikitsidwa, Mpingo wa Mzimu Woyera, iwo analekana ndi mipingo yawo yonse ndi china chirichonse, kuti atuluke kuti adzalandire ubatizo wa Mzimu Woyera. Ndipo iwo anali kuyembekezera pamenepo, "Kodi ife tichite chiyani? Mbuye wathu anakwera Kumwamba, koma Iye anatiuza ife kuti tidikire pano kwa kanthawi, kuti tingokhala kwa kanthawi pang'ono, Iye ankati atitumizire ife Chinachake choti chidzatidutsitse ife." "Oh, ndiri ndi njala kwambiri," anatero Petro, "kuti amuwone Iye."

Yohane anati, "Oh, Petro, iwe ungachite chiyani utamuwona Iye?"

143 "Mai! Chabwino, ine ndingati, 'Oh, ine ndikupepesa kuti ndinamukana Iye kunja uko. Ine sindidzachitanso izo.'" Ndiye, zonse mwadzidzidzi, apo panadzabwera kuchokera Kumwamba mkokomo ngati mkokomo wa mphepo yamphamvu, unatsika pansi.

144 Osati mwamuna wina wa Chiroma wokhala ndi kolala yake yotembenuzidwa kumbuyo, kubwera kudzawapatsa iwo mkate, kapena mtundu wina wa mgonero. Osati mlaliki wina wa Chiprotestanti kunena kuti, "Ine ndikukupatsani inu dzanja lamanja la chiyanjano, ndipatseni ine miyezi sikisi ya kuyesedwa. Kuika dzina lake pa bukhu." Ayi, ayi. Chabwino, umo ndi momwe ife tikumachitira izo lero.

145 Koma, m'bale, ine ndikukuuzani inu, izo zinali ngati mphepo yamkokomo yamphamvu, inabwera kuchokera Kumwamba, inadzazadza nyumba yonse imene iwo anakhalamo. Aleluya! M'bale, nyumbayo siyinali yaikulu mokwanira kuti iwasunge iwo. Kunja mmisewu iwo anapita, akuimba, akulumpha, akuvina.

146 Ndipo dikirani miniti, mlongo, namwali Maria anali mmenemo, nayenso. Inde, iye anali, kuchita ngati iye anali woledzera. Kodi inu mungalingalire, namwali Maria? Kodi inu mungalingalire kunena zimenezo mu mpingo wa Katolika, Methodisti, Baptisti, Presbateria, kapena kwinakwake? Namwali Maria anali pansi pa chikoka cha Mzimu Woyera, akuzandima ngati winawake woledzera. Ndipo ngati Mulungu anawapanga amayi a Yesu Khristu kupita kumeneko kuti akalandire ubatizo wa Mzimu Woyera iye asanapite Kumwamba, inu simudzakafika kumeneko chirichonse chochepera kwa chimenecho. Mwinanso mukhoza kuchotsa kukhuthala mmakolala anuwo, ndi kubwera kuno. Uko nkulondola.

147 Monga Namani wokalamba, pamene Namani anapita kumeneko kuti akalandire ake. . .Elisa anamuuza iye kuti atsikire kumeneko, akasambe ka seveni, kapena kukaziviyika ka seveni. Oh, mai, momwe izo zinapwetekera kutchuka

kwake! “Uh,” anati, “kodi madzi akuntunda uko si abwinonso chimodzimodzi?”

“Kodi mpingo wanga suli wabwinonso?”

“Ayi, Mulungu anati kumusi *kuno*.”

148 “Chabwino, tsopano, M’bale Branham, ngati ife tingapite kumeneko ndipo kukakhulupirira *izi* ndi kukakhulupirira *izo,* ife tidzakhala ndi mpingo wabwino ndi kumachita ndi aliyense mwabwino, ndipo ine ndizikapereka ndalama pang’ono mu umodzi.” Ayi, bwana. Kupatula munthu atabadwa mwatsopano, iye mwanjira iliyonse sadzalowa mu Ufumu!

149 Kotero, ine ndikukhoza kumuwona iye akuyenda kunja uko, potulutsa mapazi ake mmatope, ngati mphaka mu manyuchi, inu mukudziwa, kuyenda kunja uko. “Oh, ine ndikuganiza ine ndiyenera ndikachite zimenezo,” kuzyolika pansi. Izo zivulaza kutchuka kwake. Anabwererako, akadali ndi khate lake. Mneneriyo anati “ka seveni” nthawi yake. Koma iye atatha kuchita ka seveni, khungu lake linabwera kwa iye ali woyeranso.

150 M’bale, ine ndikukuuzani inu, anthu ena amati, “Ine sindikhulupirira kuti ine ndiyenera kupita ku guwa, ndi kukalira ndi kumafuula pamenepo, mamina pamenepo monga ena onsewo amachitira.” Kakhaleni kumbuyoko ndiye.

“Ine nditenga njira ndi onyozeka ochepa a Ambuye. Ine ndayamba ndi Yesu. Ambuye, mundipyoletse ine!”

151 Uthenga wakale uwu wandigwirizira ine, m’bale, pamene ine ndinali kuyima pamenepo pamaso pa madokotala. Iwo unandigwirizira ine pamene wamisala ankathamangira pa nsanja, nkudzati, “Ine ndimupha iye usiku uno.” Iwo unayima pafupi ndi ine mu ma ora a mayesero, pamene ndege zatsika pansi, ndipo oyendetsa ndege ali oyera pamaso pawo. Uthenga wakale uja unayima pafupi ndi ine pamene adokotala anati, “Iye ali ndi mphindi zitatu kuti akhale ndi moyo.” Iwo unayima pafupi ndi ine pamenepo, Iwo ndi wabwino tsopano. Aleluya! Ine ndikuwukondabe Iwo. Sindingakhoze kupeza zokwanira za Iwo. Uko nkulondola.

152 Chabwino, kodi izo zikuimira chiyani kwa ife? Chabwino, pamene iwo onse analedzera pa Mana atsopano awa! “Huh?” Eya, kubwera kuchokera Kumwamba. Tsopano, Mose sananene kuti, “Kaphikeni mikate yowonjezera usikuuno.” Analibe kanthu kophikira nako. Iwo anali alendo, iwo anali—iwo anali amwendamnjira ndi alendo, ndipo kotero iwo analibe kanthu koti aziphikira nako. Ndipo Mulungu ankavumbitsa iwo kuchokera Kumwamba. Ndi kulondola uko? Ndipo pamene Mulungu amavumbitsa iwo kuchokera Kumwamba, Iye anavumbitsa Mzimu Woyera kuchokera Kumwamba.

Chabwino, inu mukuti, “Tsopano, kodi Mose ananena chiyani kumbuyo uko?”

153 Iye anati, “Aroni, ine ndikufuna anyamata inu mupite kumeneko.” Tsopano mukavale majekete anu tsopano. Chabwino. “Ine ndikufuna anyamata inu kuti mupite kunja uko, ndipo mukatitengere ife ma omeri odzadza aakulu angapo. Ndipo ine ndikufuna kuti inu mukatengere izo mkati ndi kukasunga izo, mukazibwezeretse izo.” Izo zinkasungidwa Mmalo oyeretsetsa. Izo sizinkawonongeka. Izo zinkasungidwa Mmalo Oyera.

Anati, “Izi ndi za chiyani?”

154 “Chabwino, monse kudutsa mmibadwo yanu yonse, wansembe aliyense yemwe ankadzodzedweratu kuti adzakhale wansembe amene amabwera Mmalo Oyera, kuti ukakhoze kulowa mmenemo ndi ma omeri awa ndi kukatenga mana ena apachiyambi, ndi kutulukamo ndi kudzayika izo pa lirime lake, ndi kumulola iye kuti alawe, chifukwa iye amakhala woyenera, iye ndi wansembe ndipo tsopano amabwera kuseri kwa chophimba, ‘Tsopano inu mudzakhala ndi kulawa kwa mana a pachiyambi amene ankagwa pachiyambi.’” Ndicho chimene iye ankanena. Ndi kulondola uko? Ndipo ndizo zimene zinkapita kudutsa mu m’badwo.

155 Tsopano, izo ziri ndi chochita chanji ndi Pentekoste? Oh, ndipo iwo onse anali akudya mana abwino amenewo, ndipo kukuwa ndi kufuula, ndi kumapitiriza kunja uko ngati gulu la—la anthu oledzera. Bwanji, wina anati, “Kodi ife tichite chiyani?”

156 Petro anati, “Lapani, mmodzi aliyense wa inu, ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu kwa chikhululukiro cha machimo anu, pakuti inu mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera. Pakuti lonjezo liri kwa inu, ndi kwa ana anu, ndi kwa iwo amene ali kutali, ngakhale onse amene Ambuye Mulungu wathu adzawayitana.” M’bale! Aleluya! Munthu aliyense amene amakwaniritsa zofunikira za Mulungu ndi kudzakhala wansembe, kuti azikalowa kuseri kwa chophimba ndi kudzilekanitsa yekha kwa dziko lapansi, amalandira, osati kokha zodzadza mkamwa, koma mtima wodzaza ndi Manna apachiyambi amene anagwa pa Tsiku la Pentekoste. Osati chinachake *chowoneka* ngati Iwo, koma china cha Chinthu chenicheni! Aleluya! Ulemelero kwa Mulungu! Kulondola! Apo iwo anapita, akungosunthira chitsogolo. Kodi Iwo ukhala motalika bwanji? Mpaka Yesu adzabwere. Mana anakhalabe mpaka iwo atafika ku dziko linalo ndipo anatenga chimanga china chakale. Ndi kulondola uko?

157 Tsopano, kodi ife tiri ndi nthawi yanji? Oh, pepani. Ine ndachedwa ndi maminiti twente-faivi okha. Mai, izo ndi zachirendo kuti ine ndidutsitse malire mochuluka chomwecho, sichoncho izo? Chabwino, mu kamphindi chabe. Chabwino, ine ndiri ndi maminiti enanso faivi, ndipange izo kukhala theka la ora mofanana. Bwanji zimenezo? Chabwino.

158 Tiyeni tifike apa ndi kugunda mutuwo mwamsanga ndithu, iwo anali atadutsa mu chipululu. Tayang'anani pa anthuwo, monga momwe izo ziliri lero. Atumiki, osati mukhumudwe. Taonani apa, basi monga . . . Koma kumbukirani, ong'ung'udza amenewo, palibe mmodzi wa iwo amene anakalowa mdziko linalo, palibe mmodzi wa iwo. Koma iwo anang'ung'udza ndi kudandaula. Iwo anali atasiya miphika ya gariki ya ku Igupto, ndipo anali akudya chakudya cha Angelo, ndi kumadandaula za zimenezo. Si kulondola uko?

"Chabwino, M'bale Bill, ine ndikukuuzani inu, moona mtima, ine sindikudziwa chimene ine nditi ndichite. Mwamuna wanga andisiya ine." Musiyeni iye achoke.

Inu mudzilekanitse kwa chirichonse. "Iye amene sadzasiya ake omwe, ndi kukakamira kwa Ine, sali woyenera Ine."

"Ine sindikudziwa zomwe Amayi anganene." Kodi inu mumasamala chiyani zomwe Amayi anena? Ndi zomwe Yesu ananena! Mukuona? Inde.

"Chabwino, ine ndikuwopa kuti bwalo langa la zosoka lisweka." Chabwino, lisweni ilo. Uko nkulondola.

"Oh, gulu langa la zolemba, zinthu zina zonse izi! Ndine wa Makolo-Aphunzitsi ndi zonse izi. Bwanji ngati ine nditafika kumeneko ndi kuyamba kufuula?" Chabwino, fuulani.

159 Bambo wachikulire nthawi ina, iye anadzazidwa yense ndi Mzimu Woyera, inali nthawi yodabwitsa bwanji yomwe iye anali nayo. Wake—mwana wake wamkazi, amakhala naye iye. Iye ankatenga Baibulo ndi kumawerenga, kenako iye amadzuka ndipo iye nkumangolira, ndi kumayenda chokwera ndi chotsika pansi. Iye anali woti akhala ndi limodzi la maphwando ang'ono a tiyi wapinki awa, inu mukudziwa, kotero iye anamutenga bambo wokalambayo, kotero iye anati, "Ine ndimukonza iye." Iye anati, "Bambo, pali akazi amene akubwera lero." Anati, "Ine ndikudziwa kuti inu kuti simukufuna kupusitsidwa ndi akazi amenewo."

Anati, "Ayi."

Anati, "Ine ndikupatsani inu bukhu labwino kuti muwerenge." Anati, "Inu mukwere pamwamba ndipo muzikawerenga pamene ife tikuchita phwando lathu."

Anati, "Chabwino."

Anati, "Iye sadzapeza kalikonse mmenemo koti afuule nako."

160 Kotero iye anafika pamwamba apo, ndipo iye anamupatsa iye jogarafe. Kotero iye anafika pamwamba pamenepo ndipo anayamba kutembenuza masamba, iye anati, "Hum, Europe, Asia." Anapita kumeneko, anati, "Nyanja." Iye anayang'ananso pansi, anati, "Aleluya! Aleluya! Aleluya!" Anayamba kulumpha.

Ndipo atsikanawo anati, "Chabwino, chikuchitika ndi chiyani?"

Anati, "Oh, chinachake chawavuta abambo. Ife tiyenera tithamangireko." Mmwamba masitepe iwo anapita, anakwera pamwamba apo.

Iye anafuula, "Ambuye alemekezeke! Aleluya! Aleluya!"

Iye anati, "Adadi, chavuta ndi chiyani?"

161 Anati, "Oh, wokondedwa, inu munandipatsa ine bukhu labwino ili kuti ndiwerenge, ndipo ine ndinawerenga apa pamene linati nyanja ilibe popondera. Ndipo Yesu anati anaika machimo anga mu nyanja ya kuiwala, akhale kwanthawizonse. . ." Anati, "Iwo akupitabe. Aleluya! Aleluya! Aleluya!" Izo nzoona. Ndithudi, akupitabe, ilibe popondera. Anaziwona izo pamwamba apo, iwo anangotsikira pansi, nkumapitirira, oh, mai, amangopitirira nazo. Aleluya! Uko nkulondola.

162 Kudandaula, kung'ung'udza nthawizonse, "Ine sindikudziwa choti ndichite." Oh, mai, kung'ung'udza! Anasiya miphika ya gariki, kuti azidya chakudya cha Angelo. Anawasiya asing'anga odzibwekerera a ku Igupto, kuti akakhale ndi Sing'anga Wamkulu. Anasiya gulu la anthu amene ankanena kuti "masiku a zozizwitsa anapita," mai, kalanga, kukakhala ndi anthu amenewo kumene zozizwitsa ndi zinthu zonse ndi zotheka. Kukhala ndi gulu limenelo, kumadandaulabe! Uko nkulondola. Ndi chikhalidwe chotani! Iwo anasiya madzi amatope a ku Igupto, kuti akamwe mu Kasupe yemwe samauma nkomwe. Kumangodandaulabe. Nzosadabwitsa kuti thandizo lawo linadulidwa.

163 Ndiro lomwe liri vuto lero. Thandizo ladulidwa chifukwa inu mukung'ung'udza kwambiri. "Nanga bwanji ntchito ya madikoni? Mpingo wanga umati. . ." Oh, siyani, m'bale! Yang'anani kwa Khristu! Iwo anatsatira. . .

Ndiye, chinthu choyambirira inu mukudziwa, Mose anati, "Abweretseni iwo kuno. Abweretseni iwo kuno."

164 Ndipo Mulungu anati, "Yankhulani kwa Thanthwe, ndipo Ilo litulutsa madzi Ake." Ndipo pamene iye anayankhula kwa Thanthwelo. . .Tsopano, iye anatenga, poyamba, ndipo anakantha Thanthwe limenelo ndi ndodo. Ndipo pamene iye anakantha Thanthwe limenelo, ndodo imeneyo inali ndodo ya chiweruzo cha Mulungu. Iyo siyinali ndodo ya Mose. Mulungu amaigwirizira, anali naye Mose mdzanja Lake.

165 Ndipo chimene ndodo ija inali mdzanja la Mose, ndi Dzina la Yesu mu mpingo lero. Ndiko kulondola. Ndicho choonadi, m'bale. Ngati Aigupto aja akanatha kutenga konse ndodoyo kuchokera mdzanja lake, iye akanakhala wopanda mphamvu. Ngati iwo angakhoze konse kuchotsa Dzina la Yesu pa mpingo,

ndi kukuchotsanipo inu; inu mudzatuluka kumeneko ndi kukachitira mwano Ilo ndi kuliseleula Ilo, ndi china chirichonse, ndi kuyesera kubwera mmenemo ndi kudzapemphera mwa Ilo. Inu simungakhoze kuchita zimenezo. Muyenera kulisunga Ilo lopatulika! Ndiko kulondola.

166 "Oh, tenga Dzina la Yesu nawe, mwana wachisoni ndi watsoka. Pamene mayesero pozinga inu asonkhana, pumani Dzina loyera ilo mu pemphero." Ziwanda zidzabalalika, ngati mphemvu pansi pamene nyali yayatsidwa. Zoonadi.

167 Ndi awa apa. Mai! Iye anati, "Abweretseni iwo kunja uko." Ndipo iye anatenga ndodo ya chiweruzo iyi, ndipo iye anakantha Thanthwe. Ndipo pamene iye anagunda Thanthwelo, munali mphanga m'mbali mwa Thanthwelo.

168 Ndipo Thanthwe limenelo linali Khristu Yesu. Mathokozo akhale kwa Mulungu! Ndi chiweruzo cha Mulungu kwa inu ndi ine, wochimwa woyipa, woyenera imfa, woyenera kulekanitsidwa. Chiweruzo cha Mulungu chinali, "Tsiku limene inu mudzadya umenewo, tsiku limenelo inu mudzafa." Ndipo chiweruzo Chake chinamukantha Iye pa Kalvare, ndipo pamenepo Iye anapachikidwa, akuwukha magazi, akulira, akufa. Mwanawankhosa wa Adamu atapachikidwa pamenepo, Mwanawankhosa wa Abele, kani, Mwanawankhosa wophedwa kuchokera ku maziko a dziko lapansi.

169 Ndipo kuchokera pamenepo, fanizo lokongola kwambiri. Kodi iyo inakwezedwa chifukwa cha chiyani, njoka ya mkuwa? Kwa machiritso. Chifukwa cha pawiri. Pamene iwo ankasowekera kuchiritsidwa, iwo ankanyamula njoka ya mkuwa. Chinali chiyani chimenecho? Chifukwa chakuti iwo anali kung'ung'udza, kumamutsutsa Mulungu ndi Mose. Ndipo izo zinali chifukwa cha pawiri, pakuti iwo anali kung'ung'udza, amachimwa, ndipo amadwala ndipo ankasowa machiritso.

170 "Ndipo Mose," monga Yesu ananena, "monga Mose ankakwezera njoka ya mkuwa mu chipululu," kwa cholinga chomwecho, chifukwa chomwecho, chitetezero chomwecho, "chomwechonso Mwana wa munthu ayenera kukwezedwa mmwamba," chifukwa cha pawiri, "kudzapulumutsa moyo wanu."

171 Ndipo Thanthwe lokanthidwa limene linkatulutsa madzi, limene linkageyera mdziko, kuti likapulumutse anthu amene amafa. "Mulungu anakonda dziko lapansi," mu Chipangano Chatsopano, choyimira cha izo, chotsutsa, kani, "Mulungu anakonda dziko lapansi kotero kuti anapatsa Mwana wake wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira mwa Iye asatayike, koma akhale nawo Moyo wosatha." Ndi zimenezotu pamenepo. Monga izo zinali za anthu owonongeka, akufa, opanda thandizo, mwakuti njoka ya mkuwa inkakwezedwa mmwamba, Thanthwe lokanthidwa linkakanthidwa kuti likapereke Moyo ndi

machiritso ndi mtendere, kwa anthu amenewo, kotero Mulungu anamukweza Mwana Wake kuti inu musadzawonongeke, koma mudzakhale nawo Moyo wosatha. M'bale wanga, mlongo, ine ndikupemphera kuti inu mumulandire Iye usikuuno.

172 Mundikhululukire kuti ndawanyawanya phunziro langa. Ine—ine ndakhala ndisakulalikira kwa nthawi yayitali. Mundikhululukire ine chifukwa cha kutengeka kwanga, koma momwe ine ndikumverera bwino! Ndipo inu mundikhululukire ine. Ine ndikhazikika pansi masiku angapo, kuti ine ndikhoze kuphunzitsa.

173 Usikuuno, Mngelo yemweyo wa Mulungu yemwe wajambulidwa pa pepala limenelo ali pomwe pano pa nsanja iyi. Ndi chiyani Icho? Ndi Mngelo wa pangano. Ndi Ambuye Yesu Khristu akudzizindikiritsa Yekha. Ambuye akudalitseni inu. Mulole inu mumulandire Iye tsopano ngati Mpulumutsi wanu. Ine ndikuyembekezera kuyitanira kuguwa kwanga, mpaka Mzimu Woyera utandipatsa ine chitsogozo kuti ndichite zimenezo. Mukuona?

174 Ine ndikukhulupirira Mulungu adzaudzaza mpingo uwu ndi Mzimu Woyera, mpaka inu mudzamva kukuwa kumene—kumene kudzazungulira kudutsa Jeffersonville kuno. Ine ndikuyembekezera ndi kupemphera, usana uliwonse ndi usiku, ndikudikirira basi nthawi yovuta kwambiri. Inu mupitirize kusala, mupitirize kupemphera; muziwasonkhanitsa ana pamodzi, muchotse machimo onse pozungulira nyumba yanu, monga Yakobo ananena, "Chotsani ndolo zanu ndikuchapa zovala zanu." Konzekerani! Oh, ine ndikumva phokoso la mvula yochuluka!

Ambuye akudalitseni inu tsopano. Yang'anani kwa Mwanawankhosa wa Mulungu, pamene ife tikuweramitsa mitu yathu.

175 Atate athu Akumwamba, mpingo wokongola umenewo ukusuntha mu zida zathunthu! Ndipo zovala zawo sizimang'ambika nkomwe, nsapato zawo sizimachoka nkomwe pa mapazi awo. Zaka forte mu chipululu, ndipo panalibe mmodzi wofooka pakati pawo. Popanda madokotala, madokotala a padziko lapansi; basi Sing'anga Wamkulu. Popanda ulusi, popanda kanthu koti apangire zovala; koma Mlengi wamkulu anali pamenepo amene amasamalira zovala zawo kuti zisang'ambike. Iwo ankayenera kudutsa mmadzi akuya ndi mchenga wamoto, akudutsa mminga ndi mmapiri okhuthala. Chirichonse chinali mu njira, koma Lawi la Moto lalikulu lija linali kutsogolera njirayo.

176 Patsogolo pathu, sunthani, O Nyenyezi Yammawa, titsogolereni ife ndi kutilondolera. Tikhululukireni ife machimo athu ndipo tithandizeni ife kukhala antchito Anu, Ambuye. Mutenge Mawu ochepa awa omwazikana omwe ine ndayima

nawo pano, Ambuye, powerenga kuchokera mu Mawu Anu, ndipo ine ndikupemphera kuti Inu muwamize Iwo mwakuya mu mtima uliwonse. Ndipo mulole Iwo asawonongeke konse, koma mulole Inu muwapatse iwo Moyo Wamuyaya.

177 Ndipo pamene ife tiri ndi mitu yathu yoweramitsidwa, kodi alipo munthu muno, (ndi diso lirilonse lotsekedwa), kodi mungakweze dzanja lanu, ndikuti, "M'bale Branham, chonde mundikumbukire ine. Ine—ine ndatayika, ndipo ine—ine—ine sindikumudziwa Yesu ngati Mpulumutsi wanga. Ine sindinabadwe mwatsopano. Ine ndikufuna kuti inu mundipempherere ine"? Kodi inu mungakweze dzanja lanu—dzanja pakali pano? Kwezani dzanja lanu kuti ine ndikhoze kupereka pemphero. Mulungu akudalitseni inu. Ambiri a inu mwakweza manja anu mmwamba, konsekonse mchipinda chino. Izo ndi zodabwitsa. Mulungu akudalitseni inu, konsekonse. Tsopano nenani, "M'bale Branham, ine ndikudziwa, ngati Mulungu angati ayitane solo yanga, nyongolosi ya Moyo imeneyo siyili mwa ine. Iyo siyiri mwa ine. Ine sindikumudziwa Iye mwanjira imeneyo. Ine—ine kwenikweni sindikumudziwa Iye mwanjira imeneyo. Ine sindinayambe ndabadwa mwatsopano kwenikweni, koma ine ndikufuna ndikhale. Ine ndikufuna kuti ndikhale, ndipo ndikufuna kuti inu mundipempherere ine." Kodi mungakweze dzanja lanu tsopano, winawake mungakweze dzanja lanu? Pafupifupi manja dazeni. Chabwino, zikomo inu. Mulungu akudalitseni inu, mlongo. Ndipo wina wakenso. Chabwino. Tsopano, Mulungu akudalitseni inu, ndi inu, ndi inu. Chabwino.

178 Tsopano, winawake muno yemwe akufuna kuti akumbukiridwe mu pemphero, inu mukudwala, ndi kuti, "M'bale Branham, ndikumbukireni ine, ine ndikudwala." Ife sitinakhale nawo msonkhano wa machiritso, chifukwa ife tikuziwerengera izo zonse mu Uthenga, koma ine ndimapempherera odwala. Tsopano, ngati inu mungakweze dzanja lanu, nenani, "Ndikumbukireni ine, ine ndikudwala, M'bale Branham." Chabwino, awo ndi manja angapo ali mmwamba kachiwiri, amene akudwala. Chabwino, pamene ife tiri ndi mitu yathu yoweramitsidwa.

179 Ambuye, chonde mpulumutseni wochimwa ameneyo, Ambuye, wobwerera mmbuyo; perekani izi, Ambuye. Abweretseni iwo kunyumba usikuuno ndikuwadyetsa iwo bwino. Mulole iwo achoke kuchokera pano usikuuno ndi kukakonzanso pangano lawo. Mulole wochimwa wosauka uyo, mulole pilo wake akamumve ngati miyala usikuuno, iwo akalephere kupumula basi. O Mulungu, izo nzoyipa, izo zikuwoneka ngati, kuti munthu azipemphera monga chomwecho. Koma, O Mulungu, chirichonse, musalole kuti solo yake itayike. Ndizo, ngati. . .nanga bwanji ngati iye akanapita kunja kwa dziko lino, Ambuye, popanda kukudziwani Inu! Oh,

ine ndikupemphera kuti Inu mukhale naye iye. Muthandizeni mwamunayo, muthandizeni mkaziyo, nayenso, Ambuye, aliyense.

180 Ndipo tsopano odwala pano, Ambuye. Mulole, monga Mose ananyamulira mmwamba njoka ija, ndipo aliyense amene anayang'ana pa serpenti...Njoka siyinayambe yamupempherarapo aliyense. Iwo ankangoyang'ana ndi kukhala moyo, iwo ankayang'ana ndi kukhala moyo. Ndipo aliyense yemwe ankayang'ana, amakhala moyo. Ambuye, mulole odwala ndi osautsika a izi, omwe ali mchipinda chino usikuuno, ayang'ane ku Mtanda kutaliko, amuwone Kalonga wa Mtendere uja atapachikidwa pamenepo; Choyimira chotsutsa cha serpenti, chimafanana ndi njoka ya tchimo, ndipo Iye anapangidwa tchimo chifukwa cha ife. Ambuye, ine ndikupemphera kuti Inu mumuchize aliyense wa iwo pakali pano. Mulole Mzimu Woyera usunthe kudutsa pamenepo, udzadutse mwamphamvu mu umunthu wawo pakali pano, ndi kuwachiritsa iwo ku kufooka kwawo.

181 Muwadalitse iwo, Ambuye, amene ali panjira, amuna apaulendo. Amuna ndi akazi okalamba pano omwe anamenyera nkhondo kuti apambane mphotho, ndipo anadutsa nyanja zamagazi, anaima chizunzo chowawa ndi mavuto apakhomo, ndi chirichonse, ndi kumangogwedezekabe. O Nyenyezi ya Mmawa, tsogoleranibe, Ambuye Yesu.

182 Ena a masiku aulemelero awa chombo chathu chachikulu chidzachoka padoko kutsidyako. Ife tidzamva ngalawa yakale ya Ziyoni ikuwomba pamene ikubwera ndikudutsa chifunga, mchipindamo, pamene imfa idzakhazikike mwa ife ndipo okondedwa athu akukuwa. Ife tidzamumva iye akuwomba. Aleluya! Adzayenda pansi kudutsa chifunga chimenecho, mpaka pafupi ndi kama, ndipo ife tidzaponda mapazi athu pamenepo, tikafike kutsidya uko mu Dziko ilo kumene ife sitidzakalamba konse. Ndipo makwinya adzachoka pankhope. Aleluya! Tsitsi la imvi lidzachokapo. Ndipo ife tidzakhala nalo thupi ngati Thupi Lake Lomwe laulemerero. Ife tidzamuwona Iye monga Iye aliri, ndi kudzakomana ndi okondedwa athu mu Dziko losangalatsa ilo. Apatseni iwo kulimbika mtima.

183 O Mulungu, sunthirani pa mzinda uwu, ndipo mutumize mkati ochimwa, kuti pakhoze kukhala chitsitsimutso chachikulu cha solo. Perekani izi, Ambuye. Mukhala nafe tsopano mu gawo lina la msonkhanowu. Mu Dzina la Yesu ife tikupempha izi. Ameni.

184 Ambuye akudalitseni inu. Tsopano pamene muzichoka, ine ndiwafunsa abale othandizira ngati iwo angabwere kudzatenga timabukhu tating'ono kumeneko, ndi zithunzi. (Ndipo aliyense wa iwo atenge *izi*, nayenso, m'bale wothandizira, ndi—ndi chaching'ono...ndi chithunzi pamenepo.) Ngati inu mukufuna

chimodzi. Ife sitikugulitsa mabuku, ife sitikugulitsa chithunzi. Ngati mukuzifuna izo, chabwino; ngati simukutero, ndizo basi. . . Ife tinangozibweretsa izo kwa cholinga chimenecho. Kodi abale inu mungabwere patsogolo tsopano ndi kudzazitenga izo, ngati inu mungathe? M'bale Cox ndi M'bale Fleeman, ndipo ena ayime pakhomo lirilonse pamenepo, ngati anthu azifune izo.

Ndi angati amawakonda Ambuye, nenani, "Ameni!" [Osonkhana akuti, "Ameni!"—Mkonzi]. Chabwino.

185 Ine ndikudabwa ngati mlongo yemwe ali ndi mwanayo mmanja mwake, mlongoyo, wosewera, kapena apa, ngati iye wakhala pamenepo. . . Chabwino, ngati inu muli pamwamba, bwerani patsogolo apa kamphindi chabe ngati inu mungathe, ndipo mudzatipatse ife poyambira pa limba.

186 Tsopano, kumbukirani misonkhano, ikuyamba mawa usiku, inu mukudziwa pamene ife titi tidzayambire mawa usiku? Ife tidzawatenga ana a Israeli mpaka ku Kadeshi-barnea. Ndiwo mpando wachiweruzo. Ndipo kumeneko Yoswa ndi Kalebu adzawoloka ndi kudzabweretsanso.

187 Ndiyeno, ngati Ambuye alola, Lamlungu mmawa pa awa, mafunso awa ndi mayankho, Ambuye akalola, ife tidzakhala nawo iwo.

188 Ndipo Lamlungu usiku ife tikufuna tidzawatengere ana ku dziko lakwawo. Aleluya! Yordani anagudubuzikira mmbuyo, ndipo mitsinje yamatope imeneyo inagudubuzikapo. Ndipo anakwera ku makoma a Yeriko, ndipo anafuula mokweza, ndipo makomawo anagwera pansi, ndipo iwo anatenga ulamuliro. Aleluya! Ife tizidzapenyerera chingwe chofiira pamenepo, kuchokera kwa Rahabu hule, chikulendewera pansi apo pamene iye anawatsitsira azondiwo pansi.

189 Ndiye, Ambuye akalola, sabata yamawa ife tikhoza kudzapita mpaka kupyola, mpaka mu Bukhu la Chivumbulutso, kutsika kudutsa Daniele, aleluya, ndi kukhala ndi nthawi yaulemelero, yodabwitsa. Inu mumawakonda Ambuye? Ameni. Chabwino.

190 Tsopano, ndi angati amaidziwa nyimbo iyi. . . (Tipatseni ife pang'ono, basi, *Musaiwale Pemphero La Pa Banja*. Inu mukuidziwa imeneyo?) Tiyeni tiwone ngati ife tingayimbe iyo popanda zing'wenyeng'wenye tsopano. Ndi angati akudziwa nyimbo yachikale ija apa, *Musaiwale Pemphero La Pa Banja?* Chabwino, tsopano tiyeni tiyambe pang'onopang'ono.

> Musaiwale pemphero la pa banja,
> Yesu akufuna akakumane nanu uko;
> Iye adzasamalira nkhawa zanu zonse,
> Oh, musaiwale pemphero la pa banja.

191 Ndi angati a inu amene mumakhala ndi pemphero la pa banja? Tiyeni tiwone. Inde, tsopano iye wapeza poyambira tsopano. Yemwe waipeza iyo. Tiyeni tiyesere iyo tsopano, tiyeni.

> Musaiwale pemphero la pa banja,
> Yesu akufuna akakumane nanu uko;
> Iye adzasamalira nkhawa zanu zonse,
> O, musaiwale pemphero la pa banja.

192 Nyimbo yathu yobalalitsira, *Tengani Dzina La Yesu Nawe,* inu mukuidziwa iyo, sichoncho inu?

193 Tsopano ife tingayime kamphindi chabe. Tsopano pamene ife tikuyimba ndime yoyamba, ine ndikufuna inu mutembenuke, gwiranani chanza ndi woyandikana naye wanu, ndikuti, "Dzina langa ndine *John Doe*, ndine wokondwa kuti inu munali muno mu kachisi usikuuno. Ine ndikuyembekeza kudzakuwonaninso inu." Ambuye akudalitseni inu tsopano. Koma musachoke, ife tibalalitsidwa mwachizolowezi, mwanjira yathu, basi pang'ono pokha. (Abale inu mupite ku zitseko, ngati inu mungathe.) Chabwino, tsopano.

> Tenga Dzina la Yesu . . .

194 Bwererani ndipo mukagwirane chanza tsopano, mupotoloke. Ndiko kulondola. Gwiranani chanza tsopano, pangani. Ngati inu muli ndi chirichonse chotsutsa aliyense, mubwerere ndipo mukawagwire chanza, ndikuti, "Ayi, ndife amwendamnjira limodzi."

> . . . Ilo kulikonse kumene mupita.

> Dzina lofunika, O kukoma kwakeko!
> Chiyembekezo cha padziko lapansi ndi chimwemwe cha Kumwamba; (. . .?. . . M'bale Smith, ine . . .?. . .)
> Chiyembekezo cha padziko lapansi ndi chimwemwe cha Kumwamba.

Tsopano, mvetserani mwatcheru tsopano:

> Pa Dzina la Yesu kugwada,
> Kugwa modzilambatitsa pa mapazi Ake,
> Mfumu ya mafumu Kumwamba tidzamuveka Iye korona,
> Oh, pamene ulendo wathu udzatha.

> Dzina lofunika, (Oh, Dzina lofunika!) O, O kukoma kwakeko!
> Chiyembekezo cha padziko lapansi ndi chimwemwe cha Kumwamba;
> Dzina lofunika, (Dzina Lofunika!) O kukoma kwakeko!
> Chiyembekezo cha padziko lapansi ndi chimwemwe cha Kumwamba.

195 Ndife okondwa kuti inu munali muno usikuuno. Ndikufuna kuti inu mubwerere ndipo mudzakhale nafe mawa usiku, ngati inu mungathe. Ngati inu mulibe malo a ntchito, mudzakhale nafe ife.

196 Tsopano, Eledara Steel, wochokera ku Portsmouth, Ohio, angolowa kumene, wayima apa pamzere wakutsogolo. Ife timufunsa kuti iye atibalalitse ife mu mawu a pemphero.

Chabwino, M'bale Steel.

53-0327 Israeli Ndi Mpingo #3
Branham Tabernacle
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

Voice Of God Recordings, Malawi Office
P.O. Box 51453, Limbe, Malawi

Voice Of God Recordings
P.O. Box 950, Jeffersonville, Indiana 47131 U.S.A.
www.branham.org